


KUPHUNZITSA ZA MOSE

 Chabwino. Mulungu akudalitseni inu, M'bale Neville. Mmawa wabwino, abwenzi. Ine ndimayenera kuyang'ana kamodzi pa kanthawi kuti ndidziwe ngati ndi mmawa kapena madzulo. Chabwino, ndine wokondwa kukhala pano mmawa uno. Kwatentha, ndipo ndithudi inu mwalandiridwa. Ife tiribenso nyengo ya kuphukira; ife tiri ndi chirimwe ndi chisanu kuno, sichoncho ife? Chirichonse chikuwoneka kuti chabalalika, mwanjiraina.

² Chabwino, chimene chandichedwetsa ine, ine—ine ndimakonza mnyumba. Ndipo ndimamva kumangika ndi kuphwanya mmawa uno. Ndipo ndinadzuka nthawi yabwino, koma sindimadziwa kuti mkazi amakhala ndi ntchito yochuluka chomwecho yoti achite, iwo amayenera kuwakonzekeretsa ana atatu ndipo akatero awatumize ku Sande sukulu. Oh, mai! Zambiri zoti achite, zochuluka kuposa zimene ine ndimaganiza kuti zinalipo zoti achite. Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, tsopano...” Usiku wathawu ndimagwira ntchito, ndipo—ndipo ine—ine ndinabwera kuchokera ku munda wa uvangeri kuti ndidzathandizire kukonza mnyumba, ine ndikuganiza. Mai, kodi ntchito siyovuta kuti uyigwire? Hum! Ine ndinati ndizilipira madola sarte-faivi pa sabata kuti wina azimuyang'anira mwana, ndipo panalibe amene akanachita izo.

³ Mzanga analemba kachidutswa pa pepala kuno osati kale kwambiri. Ndithudi, ichi sichikupita kumeneko. Anati anali kumtunda kuno, mtundu wina wa wandale kumtunda kuno mu Kentucky, anati iye anakhalapo ku usirikali kawiri, iye anavulala katatu, ngati ngwazi, iye anali mzika mwa oyandikana nane, iye anali atachita zinthu zambiri, anapulumsa miyoyo ya ana awiri, ndipo mmodzi kuchokera ku mtsinje ndi mmodzi kuchokera kwina kwake, anaiwala zonse zimene iye ankayenera kuchita. Ndipo potsiriza iye anaganiza, chabwino, iwo amayenera kukhala bwino ndi oyandikana nawo, iye akhoza kuimira udindo. Ndipo pamene iye anatero, mwa anthu handiredi sauzande, iye anapeza mavoti faivi. Iye anafunsa apolisi ngati angapeze mfuti kuti imuthandize kuchoka mderalo, anati, “Izo zinali zowopsya ngakhale kuti azikhala mtawuniyo.” Iye analibe abwenzi okwanira oti amuthandizire iye kuchoka mtawuniyo. Kumeneko ndi kuyamikira kwa Achimerika, chonchobe, sichoncho izo? Uko nkulondola. Mu America, ukachita zochuluka, ndi momwe umayembekezedwa kuti uzichita zochuluka. Uko nkulondola, zochuluka zimayembekezedwa kwa iwe.

⁴ Chabwino, ine ndikufuna kupereka kuyamikira kwanga mmawa uno pa mmene tchalitchi chikuwonekera mwaukhondo ndi mwabwino. Ndipo pamene ine ndimabwera, iwo anali ndi chitseko kumeneko kuti chizipereka kuyenderera kwa mpweya kwabwino. Chotero izo ndizabwino kwenikweni, aliyense amene ali mu bodi yama trastii kuno ndipo anathandizira kuyambitsa izi. Icho ndithudi chinali chabwino kwambiri, ndipo iyo ndi ntchito yabwino yaikhondo. Ine ndikuganiza M'bale Hall, ngati sindikulakwitsa, anachita zimenezo. Imeneyo ndi ntchito yabwino kwambiri.

⁵ Tsopano, nthawi yatha pang'ono, koma inu mukudziwa momwe anthu achiyero aliri. Mwaona, izo ziribe nthawi yeniyeni, kodi ife tiri nayo, M'bale Slaughter, M'bale Deitsman? [Abalewo ndi ena akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Basi chirichonse basi mmene ife tikuchitengera icho.

⁶ Tinali ndi misonkhano yopambana kumusi Kummwera! Koma ine ndinangoyankhula kwa masiku angapo apitawo. Ine ndinalalikira kwa miyezi foro, molumikiza, ndipo ndinalibe mawu okwanira kuti—kuti ndinganong'one nkomwe. Ine ndinkachita mokhala ngati kumapanga zizindikiro kwa mkazi wanga, inu mukudziwa, chimene ine ndimafuna, ndipo izo ziri ngati a . . . Ndipo kenako zitatha zimenezo, ndipo ndikubwera kuno kumene izo zinadzakhala ngati nyengo yachinyengo ife takhala tiri nayo, (bwanji, kuzizira tsiku lina ndi kudzatentha lotsatiralo), ine ndinatenga chimfine chenicheni, chachikale kwenikweni. Ndipo ine ndinadzuka, masiku angapo apitawo, ndipo ndinayamba kenanso. Ndipo chotero ndife othokoza kwa Ambuye wabwino, ngakhale, pa ubwino Wake wonse ndi chifundo kwa ife, ndi—ndi mmene Iye wakhalira wabwino. Tinali ndi misonkhano yopambana kumusi uko, ndipo Ambuye anatidalitsa ife mopitirira, mochuluka.

⁷ Ndipo usiku wathawu, kuyandikira pakati pa usiku, M'bale Wood anandiitanira ine kumusi ku nyumba yake, ndi M'bale Arganbright pa foni, amafuna ine ndikayambire ku Switzerland. Chotero, izo ndi kuyenda kochuluka kwambiri kwa munthu wokalamba.

⁸ Chotero, tsopano, msonkhano wathu wotsatira udzayamba pa leveni wa mwezi ukubwerawu, ku Cadle Tabernacle ku Indianapolis. Ku a—ku Cadle Tabernacle mu Indianapolis, kuyambira pa leveni mpaka pa ffitini. Ndipo kenako, kuchokera kumeneko, kupita ku—ku Minnea- . . . Minneapolis; kuchoka ku Indianapolis kupita ku Minneapolis, Christian Business Men.

⁹ Tsopano ine ndikuganiza M'bale Neville anandiitana ine, ndipo ine ndimafuna kuti ndiwonetse kwanga . . . kuwonetsera kuyamikira kwanga kwa iye ndi a Neville atatu amene anabwera kumusi ndi kudzandiimbira ine pa maliro amenewo, amene ndinali nawo dzana. Ndipo ine ndinamufunsa

M'bale Neville; ndinalibe oyimba aliwonse, banja la Liddick; pamene Bambo Liddick anapita Kwathu ku Ulemelero. Ndipo ine ndithudi...ngati mwana wake wamwamuna, ine sindikumuwona iye pano; ndipo ine ndinadzapeza pamapeto kuti anali mwana wongosungidwa. Akudziwa kuti abambo ake akumwalira, wosapulumutsidwa, anathamangira kunyumba kuti akanditenge ine, pambuyo iye...ndipo abambo ake anapulumutsidwa asanamwalire. Chotero chinthu chachikulu chimene mnyamatayo anachita, chinali kubwera kudzamutenga winawake woti apempherere abambo ake asanapite. Ndipo a Neville atatu anabwera kumusi ndipo anawayimbira iwo mokoma kwenikweni.

¹⁰ Ndipo chotero M'bale Neville anandifunsa ine ngati ndingayankhule mmawa uno ndi madzulo ano, kenanso. Chotero inu zindikirani, Lemba limati, "Pemphani mochuluka kuti inu..." Chotero M'bale Neville ndithudi ndi wa Mwamalemba pa zinthu zimenezo, kwambiri! Ndipo chotero ine ndichita mmene ndingathere.

¹¹ Tsopano, ine ndinati mmawa uno, pokhala ndi Tsiku la Anakubala, ndipo ife tikufuna kuti tiyankhule kwa—kwa ana aang'ono. Ine ndinaganiza mmawa uno ikhala nthawi yabwino kwa—kwa ana aang'ono. Tsopano ine ndikuganiza kuti tsiku la anakubala...

¹² Tsopano, palibepo chirichonse chokoma pa dziko lapansi, chimene ife tikuchidziwa, kuposa mzimayi weniweni, woona. Mulungu adalitse solo yake yokhazikika, weniweni, mayi weniweni. Koma ife tiri ndi alowammalo ambiri lero amene—amene amatchedwa "anakubala," amene si amayi; iwo angokhala amayi amene ali ndi ana, koma osati anakubala. Mayi wachikale ndi amene amasamalira banja lake, ndipo samakakhala pa makonde amenewo ndi kumakavina, ndi usiku wonse, kumasuta, kumamwa, kubwera mmenemo. Iye siwoyenera dzina lopatulika limenelo la mayi. Iye amangokhala mkazi basi, ndizo zonse, amene akulera mwana; koma osati anakubala, chifukwa *anakubala* ali ndi tanthauzo losiyana kwa izo. Tsopano ine—ine ndikuganiza ngati inu...

¹³ Tsopano, kwa Tsiku la Anakubala, ine ndikufuna ndizifotokoze ndekha mwabwino kwenikweni. Ine ndiri ndi amayi a imvi akhala pamenepo, inemwini. Ndipo ine ndikuganiza, tsiku, chabwino; koma tsiku lirilonse likuyenera kukhala tsiku la anakubala, basi osati kungoti kamodzi pa chaka. Ndipo chifukwa chimene zinthu izi za Tsiku la Anakubala zikuchitika tsopano...

¹⁴ Ndipo ine ndikuwona ife tangokhala ndi apang'ono, ndipo ife tonse timadziwana wina ndi mzake. Ndife abwenzi akumudzi, ndipo ndi chifukwa ife titi tiyankhule mwanjira iyi.

¹⁵ Ine ndikuganiza kuti mayi akuyenera azilemekezedwa tsiku lirilonse chimodzimodzi, uko nkulondola, mayi weniweni. Ndipo, koma tsiku ili iwo amalitcha Tsiku la Anakubala, si kanthu mdziko koma zamkhutu zazikulu zamalonda, basi kuti zizingowathera anthu ndalama. Ndipo ndi chamanyazi kwa amayi, Tsiku la Anakubala, kamodzi pa chaka, “Chabwino, ife sitimapita kukawawona iwo, koma ife timatumizira iwo mulu waung’ono wa maluwa ndipo izo zimakhazikitsa izo.” Amenewo si amayi! Mai, kalanga! Mayi weniweni ndi mzimayi amene iwe. . . m’modzi amene anakulera iwe, ndipo iwe umamukonda iye, ndipo iwe umamuwona iye ndipo umayankhulana naye nthawi zonse. Iwe umawonetsera chikondi chako kwa iye nthawi zonse, osati tsiku limodzi lokha pa chaka.

¹⁶ Koma basi ine ndisanayambe pa sewero langa laling’ono, ine ndikungofuna ndifotokoze ichi, ndi kukonzanso. . . Ena a inu, ambiri a inu munafa, ambiri a iwo anapita kuyambira pamene izi zinapangidwa. Zinali mu 1933.

¹⁷ Kodi inu munawona mu pepala mausiku angapo apitawo pamene mzimayi ameneuja anamupha mwamuna uja? anamuponyera iye kunja mu msewu wake ndipo anangobwerera mmbuyo ndi mtsogolo kumuponda iye ndi galimoto yake mpaka anangomuphwanya iye pa msewu. Ndipo iwo anati, o—oyimira mlandu ndi ena otero, anati, “Kodi zimenezo sizikudzuzula chikumbumtima chako?”

Iye anati, “Mulungu ndi ine tatopa mmene amayi akutengedwera.” Huh! Eya, iye ndi fano. Uko nkulondola. “Kufika potopa.” Fuko ili lingatsike pansu bwanji? Ife tingapite patali bwanji opanda chiweruzo cha Umulungu, ine ndikudabwa? “Mulungu ndi ine”? Ngati Mulungu akanakhala wolakwa ndi zamkutu zonse zimaikidwa pa Iye, Iye sibwenzi atakhala Mulungu, ndizo zonse. “Mulungu ndi ine”? Mai! Mulungu alibe chochita ndi zotero monga izo. Ndikudabwa pamene iye adzakhale kumeneko mu mazunzo, momwe iye adzaganizire za izo nthawi imeneyo? Oh!

¹⁸ Amerika! Tsopano inu mukukumbukira, ngati simunalembe izi, lembani. Uku ndi kulosera kwanga. Mukuona? Mu 1933, pamene ife tinali ndi misonkhano kumusi kuno kumene wakale, ine ndikuhulupirira Church of Christ chiri kumeneko tsopano, icho chinali chakale. . . Icho chiri komwe kuno, M’bale Neville, kumusi kwenikweniko molunjika. Charlie Kern ankakhala kumeneko. Nchiyani icho. . . Nyumba ya amasiye kuno pa Meigs Avenue. Mu 1933, ine nditangopeza Ford ya 1933, ndipo ndinaipereka iyo mmawa umenewo kwa Ambuye. Ndipo, ndisanachoke kunyumba, ine ndinawona masomphenya. Ine ndinawalemba iwo, pepala lachikasu lakale likudikirabe mu Baibulo. Ine ndinawona mapeto a nthawi akubwera.

¹⁹ Ndipo, inu, ndi angati amene angakumbukire mmene galimoto ya '33 inkawonekera kumbuyo uko? Oh, iyo inali yokutha monga *chonchi*, ndipo komwe kumbuyo, ndipo anadulapo kuti tayala lapadera lizipachikidwapo. Ine ndinawona masomphenya, amene, “Kudza kwa Ambuye kusanafike, kuti magalimoto azidzawoneka ngati dzira.” Ndi angati akukumbukira kuneneratu kumeneko? Alipo aliyense amene watsalira muno? M'bale Seward anapita. Ndipo ine ndikuganiza. . . Inali 1933 pamene ife tinali ndi misonkhano kuno. Ine ndikuganiza pafupifupi onse a iwo anapita tsopano, kuchokera nthawi imeneyo.

²⁰ Ndipo ine ndinaneneratu, kuti, “Amerika, mulungu wawo wa nambala-wani adzakhala mzimayi.” Ndicho chimene icho chiri. Chirichonse chikupangidwa motsanzira Hollywood. Ine ndiri ndi zinthu zosungidwa kuchokera mu failo ya FBI zimene zikhoza kukugwedezeni inu mzidutswa kungo—kungoti ndikuuzeni inu, pomwepo. . . Ndipo kuyaluka pa akatswiri amakanema awa, palibepo mmodzi wa iwo, nkomwe, koma chimene ali mahule. Ndipo a FBI aziika poyera zimenezo pompano. Ine ndiri nazo kuchokera mu failo yawo yomwe. Ndipo chotero onse a iwo akukhala kunjwa, ngakhale akatswiri amakanema awa, kumene iye anatsimikizira, iwo anapita ndipo anakawatenga iwo, akukhala ndi amuna, madola twente faivi ndi fifite usiku, mwamuna, paliponse kumtunda ndi kumusi, mu Hollywood ndi paliponse, anali ndi nyumba zapadera ndi amuna kumbuyo kumeneko kumene iwo amawatumiza iwo kunjwa uko kwa anthu awa. Ndipo ndicho chimene ife timayang'anapo, televizioni, ndi—ndi kunjwa kuno pa makanema ndi zinthu, ndi kuwalola ana athu kumamutcha iye fano. Ndipo kenako nkumutcha ameneyo *mayi*? Izo zatalikana kwambiri ndi kukhala mayi. Izo ndi nyansi. Ndizo ndendende. Ndipo komabe iwo akukhazikitsa liwiro la lero. Ife timawalola iwo. . . mtundu wa zovala zimene iwo amavala, muwawone azimayi achi Amerika atavala monga iwo, ndi chirichonse. Ndithudi. Ndipo mulungu wa Amerika ndi mzimayi. Osati Yehova; iwo achokako kwa Iye. Osati kwa *mayi* tsopano, tsopano zisiyeni izo pambali, icho ndi chinthu choyera chimene ife titachikambe; koma ine ndikutanthauza *mkazi*.

²¹ Ndipo, kumbukirani, ine ndikuneneratu kuti kuthetsedwa kwathunthu kwakukulu kusanachitike, chimene ine sindikunena kuti Ambuye andiuza ine, koma ine ndikukhulupirira padzakhala chinachake chidzachitike mwina pakati pa pano kapena pa nthawi imeneyo mu '77. Izo zikhoza kubwera pa ora lino. Koma pakati pa pano ndi '77, ine ndikuneneratu kuti mwina chiwonongeko chachikulu kapena kuthetsedwa kwathunthu kwa dziko lapansi lonse, pakati pa tsopano ndi '77.

²² Ine ndinaneneratu izo, mu 1933, ine ndinaneneratu kuti akazi adzakhala akupitirira kumaipirayipira ndipo fuko

lizidzapitirira kugwa, ndipo iwo adzakhala akukakamira kwa amayi, kapena ngati amayi monga choncho, mpaka iwo adzakhala, mkazi adzakhala fano. Ndipo patapita kanthawi, izo, “Amerika adzalamuliridwa ndi mkazi.” Mulembe zimenezo ndipo muwone ngati izo sizolondola. Mkazi adzatenga malo a Purezidenti kapena chinachake, chachikulu, mphamvu ina yapamwamba mu Amerika.

²³ Pamene, ine ndikunena izi ndi ulemu, madona, pamene mkazi achoka ku khitchini, iye amachoka pa malo ake. Uko nkulondola. Kumeneko ndiko kumalo kwake. Kunja kwa kumeneko, iye alibe malo. Ndipo tsopano, ine sindikukhwimitsa pa iwo, koma ine ndikungonena chimene chiri Choonadi ndi chimene Baibulo...Zinkakhala kuti mwamuna ndi amene amakhala mutu wa nyumba, koma zimenezo zinali mmasiku a Baibulo. Iye salinso konse. Iye ndi chidole, kapena iye ndi a...kapena wolera ana kapena chinachake. Ndipo tsopano, ayi, iwo amafuna kuti azisamalira agalu, azipanga zolera, ndi kumanyamula kagalulu kakang’ono mmanja mwawo nthawizonse, kuti muzithamangathamanga usiku wonse.

²⁴ Ndine—ine sindikukamba za amayi. Mulungu awadalitse iwo. Ndicho chimene chimagwira fuko pamodzi tsopano, theka la njira, ndi weniweni, wabwino, wopatulika, mayi wopulumutsidwa ndi Mulungu. Uko nkulondola.

²⁵ Koma manyazi a mmene azimayi athu atsikira! Ine ndiri ndi chidutswa cha pepala, ine ndinachidula ichi itatha Nkhondo ya Dziko lonse yotsiriza iyi, yachiwiri, chimene chinati, “Zikhalidwe za akazi aku Amerika zinapita kuti, kuti, atakhala miyezi sikisi kutsidya kwa nyanja, foro mwa asirikali faivi anasiidwa chikwati ndi akazi awo, ndipo iwo anakwatiwa ndi mwamuna wina?” Ndipo sakanawadikira iwo nkomwe kuti abwerere kuchoka ku tsidya la nyanja, asirikali kumeneko akufa pabwalo la nkhondo! Munthu ameneyo amene amachita zimenezo siwoyenera kutchedwa mayi, dzina lopatulika limenelo. Ayi, si choncho. Chotero ine nthawizonse ndimatchedwa “wodana ndi akazi,” koma ine sindiri. Ine ndikuganiza mkazi ndi chinthu chopambana, ndipo mayi, makamaka. Koma iwo akuyenera kumakhala pamalo awo ndipo asamatenge malo a mwamuna, ndipo asamatenge malo a Mulungu.

²⁶ Ndipo mmawa uno ine ndinamva a mpingo wa chiyero akunena, kuti, “Mayi amalamulira nyenyezi za Kumwamba,” ndi zonse izi. Ine ndikhoza kuganiza Akatolika akuchita zimenezo pa namwali Mariya, ndi zina zotero monga choncho, zimene, zopembedza amayi akufa, Cecilia Woyera ndi onse monga choncho, chimene chiri mawonekedwe aakulu a zamizimu. Ndizo zonse zimene ziripo. Chirichonse chimene chimayankhulana ndi akufa ndi zamizimu. Chotero, alipo

Wopembedzera mmodzi yekha pakati pa Mulungu ndi munthu, ndipo ameneyo ndi Khristu Yesu. Uko nkulondola. Palibe woyera wina, palibe kalikonse kunjira kwa Ambuye Yesu Khristu ndi Iye yekha Amene ali Wopembedzera pakati pa Mulungu ndi munthu. Koma pamene ine ndiwona mipingo, ngakhale zopita kuseri kwa guwa, kupatulika konse kunatengedwa kuchokera kwa Khristu ndipo kunaperekedwa kwa amayi, kupatulika konse kunatengedwa, kenako—kenako iwo amayamba ndipo ndi zimenezotu.

²⁷ Chotero, koma alipo mayi weniweni amene watsalira. Mulungu alemekezeke! Chimodzimidzi monga pamene inu muwona wonyenga; alipo Mkhristu weniweni amene amakhala moyo kwenikweni. Pamene inu muli ndi zabwino, mumakhala ndi zoyipa. Ndiko kulondola ndendende. Ndipo tsopano, mtundu wa mayi umenewo ndi mtundu wa mwana umenewo, ife tikufuna tiyankhulepo tsopano mu Baibulo.

²⁸ Tsopano ine ndikudabwa, ndi anyamata angati aang’ono ndi atsikana amene ife tiri nawo kuno mmawa uno? Ngati inu munamva kuwulutsa kwa M’bale Neville dzulo. . . Ndi anyamata angati aang’ono ndi atsikana amene angakonde kubwera kuno ndi kudzakhala pa mpando woyambirira pamene ndikuyankhula ndi inu? Inu mungakonde kubwera kuno? Pali mipando wani, thuu, firii, foro, faivi apa; wani apa, ndi sikisi, ndi mipando ina yaying’ono kuno. Kodi inu mungakonde kubwera kutsogolo, ena a inu anyamata aang’ono mukhoza kukhala opanda amayi anu, ndipo mukufuna kubwera kuno? Ndinu olandiridwa kwambiri! Amayi bwerani. . . [M’bale Neville akuti, “Alipo ochuluka; ambiri a iwo mu chipinda cha Sande sukulu.”—Mkonzi]. Oh, iwo ali mu chipinda cha Sande sukulu. Chabwino, ziri bwino. Ife tidikirira maminiti angapo, ndipo tiziyankhula, ndipo iwo akhala atatuluka mu maminiti angapo. Ndipo ife tingosonkhana mozungulira, maso aang’ono akuda, ndi a brauni, ndi a buluu, kumtunda kuno, ndi—ndi kumayankhula kwa aliyense wa iwo. Tsopano, ndi angati amawakonda Ambuye? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni!”] Chabwino.

²⁹ Tsopano ndikufuna kuti ndiyankhule ndi amayi ndi ana, ndipo izo zikulunjika kwa iwo.

³⁰ Usikuuno, ngati Ambuye alola, ndikufuna ndidzayankhule pa chozizwa choyamba chimene Yesu anachita, ndi mmene icho chinachitikira, ndipo ndi mphamvu yanji, ndi chimene Iye anachita pamene Iye anachita Chake. . . Ndi angati akudziwa chozizwitsa choyamba chimene Iye anachita? Chineneni icho, nonse pamodzi: “Anasandutsa madzi kukhala vinyo.” Uko nkulondola, chozizwitsa choyamba chimene Iye anachichita. Tsopano, ngati Ambuye alola. Pamene ine ndimawerenga, mmawa uno, icho chinangobwera mmalingaliro anga.

³¹ Ine ndikuwona tiri ndi mzathu wabwino, Bambo ndi Mayi Yeker kumbuyo uko, ine ndikukhulupirira, mmawa uno. Zinangochitika kuti ndinawazindikira iwo pamene ndimatembenuka kuzungulira chipupa mbali iyi. Tsiku lina ine ndinali ndi kupimidwa; ine ndimayenera kukonzekera kupimidwa chifukwa cha ntchito ya kutsidya kwa nyanja. Ndipo, pamene ine ndinatulukako, ndinakumana ndi ndani koma Bambo ndi Mayi Yeker, atakhala kunjira uko mu ofesi—ofesi.

³² Dr. Schoen, mu Louisville, m'bale wabwino kwambiri wa Chikhristu. Ine ndikukuuzani inu, ine ndinakumana ndithudi ndi mwamuna weniweni kumeneko, weniweni amene amakhulupirira mwa Mulungu ndipo amayika chidaliro chake mmenemo. Inu mukudziwa chiyani? Ine ndikukuuzani inu. Ine ndimapeza madokotala ochuluka akukhulupirira mu machiritso Auzimu kuposa mmene ndimapezera alaliki. Uko nkulondola. Iwe ukayankhula nawo. Amati, “Ndithudi.” Ndipo pamene iye . . . Pamene ine ndinapita kuti ndikanyamuke, iye anagwira dzanja langa, iye anati, “M'bale Branham, inu mumachita zochuluka zothandiza anthu kuposa mmene ine ndingachitire.” Iye anati, “Uko nkulondola.” Anati, “Inu mukhoza kuwathandiza anthu amene ine sindingawakhudze nkomwe.” Anati, “Uko nkulondola.”

³³ Ine ndinati, “Chabwino, chifukwa, inu mukhoza kusokelera, kapena kuyikapo fupa, kapena chinachake monga choncho. Koma Mulungu ndi amene amachiritisa.”

³⁴ Iye anati, “Uko nkulondola.” Ameni. Oh, ine ndimakonda kuwona anthu amalinaliro aakulu, oganiza mwanzeru. Ine ndimaganiza za opreshoni, ndi za dokotala wa zamakhwala, ndi a za nsana, a mafupa, machiritso Auzimu, ndi zonse pamodzi, ngati chichonse cha izo chingamuthandize aliyense, ine ndingatsatire izo. Ndipo pamene inu mumupeza dokotala akumudzudzula mlaliki; mlaliki akumudzudzula dokotala; ndipo wa zamafupa akumudzudzula—akumudzudzula wa opreshoni; wa opreshoni akumudzudzula dokotala wa zamankhwala; inu mukhoza kulingalira ichi, pali cholinga chodzikhonda penapake. Uko nkulondola, chifukwa mmodzi aliyense wa iwo watsimikizira kuti amathandiza winawake. Ndiko kulondola ndendende.

³⁵ Tsopano chenicheni chake ndi ichi, ine ndikuganiza, ngati zolinga zathu ndi zolondola, ndipo mitima yathu ndi yolondola kwa anthu, ife tonse tikuyenera kugwira ntchito limodzi kuti timuthandize munthu mzathu, kuti tipange moyo wophwekerapo. Ndipo kenako zolinga zanu sizikhala zodzikonda, muzipereka matamando kwa Mulungu Amene amapereka zinthu zonse mwaulele. Ameni. Inde, bwana. Oh,

ife tisamakhale ndi kudzikonda kulikonseko; izo zikuyenera kukhala mwangwiro.

³⁶ Ngati wa zansana angathandizire *ichi*, ndipo wa mafupa nkuthandizira *ichi*, wa opareshoni kuthandizira *ichi*, ndi chinachakenso nkuthandizira *icho*, tiyeni tizipempherera zonsezo, ameni, kuti Mulungu awathandize anthu Ake okondedwa kuti akhale bwino bwino ndi okondwa. Chifukwa, ife tiribe nthawi yayitali yokhalira kuno, basi masiku ochepa ndipo ife tikhala pa msewu, tikupita kwinkwakwenso. Chotero chimene ife tikuyesetsa kuti tichite ndi kuwupanga moyo kukhala wophwekerapo kuti muzikhala ndi nthawi yabwino pamene muli kuno. Ameni.

³⁷ Tsopano pa lingaliro ili, tiyeni tiweramitse mitu yathu tisanatsegule Baibulo, ndipo tiyankhule kwa Mpulumutsi wathu wokondedwa.

³⁸ Athu achifundo, Atate Akumwamba, ife tikubwera modzichepetsa mmawa uno mu Kukhalapo Kwanu, ndipo tikukuthokozani Inu pamwamba pa chirichonse chimene chinakhalapo pa dziko lapansi, kapena chimene chiti chidzakhalepo, kwa Ambuye Yesu Khristu. Pakuti, Iye anali Mmodzi Amene anamubweretsa munthu ndi Mulungu pamodzi, ndipo anatiyanjanitsa ife alendo osauka osayenera, opanda umulungu, otalikirana ndi Mulungu, mwa—mwa kusankha, kwa ifeeni, ife tinatenga kusankha kwathu ndipo tinayenda kuchoka kwa Iye. Ndipo Iye anali wabwino kwambiri kuti anabwera, ndipo pamene ife tinali osakondweretsa kwa Mulungu, pamene ife tinali ochimwa, otalikirana ndi Mulungu, Iye anatiyanjanitsa ife kubwera kwa Atate, kudzera mu kukhetsa kwa Magazi Ake Omwe.

³⁹ Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha Iye! Ndipo lero wayima ngati Mkhlapakati, Mmodzi yekhayo pakati pa Mulungu ndi munthu, Amene angapangitse pemphero kufika mu Kukhalapo kwa Mulungu, kudzera pa nsanja ya Magazi Ake Omwe amene Iye anawakhetsa kuchokera pa dziko lapansi kupita ku Ulemelero. Anabwera pa dziko lapansi lino mwa njira ya modyera, anabadwira mu khola. Anachoka pa dziko lapansi, podzera chirango chachikulu. Dziko lapansi silinamufune Iye. Kumwamba sikunamulandire Iye, chifukwa Iye anali wochimwa, Iye anali ndi machimo athu pa Iye. Dziko lapansi silinamufune Iye. Iwo anamukana Iye, “Chokaniko kwa Munthu ameneyo!” Iye anali ngakhale... analibe nkomwe malo oti adzabadwirepo, kapena malo oti adzaferepo. Ndipo Iye anapachikidwa pakati pa Mmiyamba ndi dziko lapansi; Kumwamba sikukanamulandira Iye, ngakhale dziko lapansi silikanamutenga Iye. Ndipo Iye anafa, mulimonse, kuti adzatipulumutse ife ku tchimo, kuti adzachize matenda athu, kuti adzatipatse ife chimwemwe ndi kukhala kokoma

pamene ife tiri pano pa dziko lapansi. Ndi Mpulumutsi bwanji! Oh, mmene ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha Iye!

⁴⁰ O Mulungu, mulole kuyamikira kulikonse kwa mtima wathu kutsanuliridwe pa Iye, ndipo Iye yekha. Mulole maulemu aliwonse ndi kupembedza kulikonse, chirichonse chochokera mmilomo yathu ndi mitima, mulole icho chiikidwe pa Iye Amene ali woyenera chirichonse, Iye Amene anakhala pa Mpando wachifumu tsiku lina, ali ndi Bukhu mdzanja Lake. Palibe munthu Kumwamba kapena padziko lapansi anali woyenera kapena wokhoza ngakhale kuti ayang'ane pa Bukhulo, kapena kumasula Zisindikizo zimene zinasindikiza Ilo. Ndipo Mwanawankhosa uyu amene anaphedwa, maziko a dziko lapansi, anabwera, analitenga Ilo kuchokera mdzanja Lake, anadzatzegula Zisindikizo ndipo anamasula a—Mawu, kwa anthu.

⁴¹ Ndipo, Atate, ife tikupemphera lero kuti Mzimu Wake Woyera umasule mitima yathu kuchoka ku mdima wake wonse, umasule lirime lathu ku zonse zimene ziri zoipa, khululukirani machimo athu onse, ndipo muchotsepo mdima wonse, ndipo musunthire mmitima yathu mmawa uno.

⁴² Ndipo makamaka ana aang'ono awa, Mulungu, adalitseni iwo pamene iwo akhala pano mmawa uno ndi amayi awo okondedwa. Mulungu, momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha umayi, chifukwa cha amayi enieni! Pakati pa mdima wonsewu ndi kupembedza mafano, ndi nyansi ndi chivundi cha mdziko, komabe ife tiri ndi enieni, amayi enieni. Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha iwo! Aang'ono ndi aakulu, onse awiri ofanana, ife tikukuthokozani Inu, Atate, chifukwa cha umayi weniweni. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu muwadalitse iwo.

⁴³ Kuwawona, atakhala pano mmawa uno, ambiri a abale athu ndi alongo avala marozi oyera kapena maluwa oyera ndi maluwa, kutanthauza kuti amayi awo oyera okondedwa anawolokera kuseri kwa chophimba, mbali inayo; osati anafa, koma amoyo kwa nthawizonse. Tsikulina iwo adzabwera, aponso, kumusi pa mtsinje, ndipo kumeneko iwo adzawawona iwo kenanso, mbali inayo. Ambiri avala marozi ofiira, amayi akadali kuno. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha izo.

⁴⁴ Ndikupemphera kuti Inu mutidalitse ife pamodzi pamene tikuwerenga Mawu Anu, pakuti tikupempha izi mu Dzina la Khristu. Amenii.

⁴⁵ Tsopano Ambuye akudalitseni inu. Ndipo tiyambira pa Mawu mmawa uno. Tsopano, poyamba, sewero laling'ono ili lisanafike, ine ndinaganizira za amayi ndi ana aang'ono... Ndipo iwo mwinamwake andimva ine, chifukwa chinthu ichi chiri ndi mawu ndithu. Ndipo ndipanga sewero pang'ono, chifukwa ndakhala ndikuzindikira tsopano misonkhano yanga,

nthawizina masewero amathandizira chinthu chonsecho. Kodi inu simukuganiza choncho? Anyamata aang'ono amazimvetsa izo bwino. Ine ndikuyang'ana pa gulu la anyamata aang'ono, amaso owala akhala pansa, akundiyang'ana ine tsopano, amene adzakhale amuna a mawa ngati kuli mawa.

⁴⁶ Ndipo tsopano tisanakhale ndi sewero lirilonse, kapena china chirichonse chimene chikuchitika mu mpingo, icho chikuyenera kukhala ndi maziko a Baibulo. Amen. Icho chikuyenera kukhala maziko a Baibulo. Poyamba, tiyeni ife tonse titsegule ku Mateyu, mutu wa 16 ndipo ndime ya 25, ndipo ife tiwerenga ndime izi. Poyamba, pamene ife tikuwerenga, kukonzekera, mwinamwake pa nthawi imeneyo anyamatawo akhala atatuluka. Tsopano Mateyu 16:25, ife tikuwerenga izi:

Pakuti aliyense amene adzasunga moyo wake adzawutaya iwo: ndipo aliyense amene adzataye moyo wake pa chifukwa cha ine adzawupeza iwo.

⁴⁷ Tsopano, ili ndi Lemba lofunikira kwambiri. Tiyeni tonse tiwerenge izo pamodzi. Inu mukuti chiyani? Aliyense, ana aang'ono ndi nonse, pamodzi tsopano. [M'bale Branham ndi osonkhana akuwerenga Lemba lotsatirali pamodzi—Mkonzi].

Pakuti aliyense amene adzasunga moyo wake adzawutaya iwo: ndipo aliyense amene adzataye moyo wake pa chifukwa cha ine adzawupeza iwo.

⁴⁸ Inu mukudziwa, anyamata ndi atsikana, ndipo ine ndikudziwa aakulu asangalala ndi ichi basi chimodzimidzi momwe ana ati achitire. Koma, Lemba limenero ndi lofunikira kwambiri! Ndipo Malemba ena ndi ofunikira kwambiri mpaka Mulungu anawayika iwo mu Mauthenga anayi onse: Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane. Koma, ili linali lofunikira kwambiri mpaka Iye analiyika ilo ka sikisi mu Uthenga! Ka sikisi izi zinabwera kuchokera pa milomo Yake Yomwe, Yesu.

⁴⁹ Tsopano mu Marko, ife titsegula mmenemo, pa mutu wa 8 wa Marko, ndipo tiyambira ndi ndime ya 34, ndipo ndiwerenga zina pamenepo. Ndipo ndikufuna inu muzindikire apa kenanso, ndi kupitiriza pang'ono kwa izi pamene Yesu ankayankhula izo. Ndipo kumbukirani, Iye anaziika izo ka sikisi mu Uthenga, kuti zikhale zotsimikizika! Thuu ndi mboni, koma Iye anayika izo katatu kuti, mwaona, kuti zikhale zotsimikizika kuti inu muzikumbukira izo.

Ndipo pamene iye anali—pamene iye anawayitana anthu kwa iye ndi ophunzira akenso, iye anati kwa iwo, Aliyense amene adzanditsatira ine, muloleni iye adzikane yekha, . . . atenge mtanda wake, ndipo anditsate ine.

⁵⁰ Tsopano, mmodzi wa womasulira analemba, “Atenge mtanda wake ndi kunditsatira Ine tsiku ndi tsiku.” Tsopano, tsopano ndime ya 35. Mvetserani:

Pakuti aliyense amene adzasunga moyo wake adzawutaya iwo; koma aliyense amene adzataye moyo wake chifukwa cha ine ndi uthenga, yemweyo adzawusunga iwo.

Pakuti chidzamupindulira chiyani munthu, ngati iye angapindule dziko lonse, ndi kutaya solo yake yomwe?

Kapena munthu adzapereka chiyani posinthanitsa ndi solo yake?

⁵¹ Tsopano tiyeni titenge ndime ya 35 iyi ndipo tiibwereze iyo pamodzi tsopano. Chabwino. Tsopano tiyeni tinene iyo pamodzi. Ife titenga Marko 8:16, tsopano tiyeni tinene iyo limodzi; Marko 8:16, mundikhululukire, Marko 8:16, 35. Ayi, ndalakwitsa izo. Marko 8, mundikhululukire ine. Marko, Marko Woyera, mutu wa 8, ndime ya 35. Tsopano tiyeni tiyesere izo. Marko Woyera, mutu wa 8, ndime ya 35. Tsopano ife tayipeza iyo. Tiyeni tiweringe iyo. [M’bale Branham ndi osonkhana akuwerenga Lemba lotsatirali pamodzi—Mkonzi].

Pakuti aliyense amene adzasunge moyo wake adzawutaya iwo; koma aliyense amene adzataya moyo wake pa chifukwa changa ndi chifukwa cha uthenga, . . . adzawusunga iwo.

⁵² Izo nzopambana? Tsopano, ife tifika pa nkhani yathu yaying’ono, ndipo pamene ana akubwera iwo adzatenga malo awo. Othandizira muziwayang’ana iwo pamene iwo, mwakachetechete. . . inu muwone ngati mungawalowetse iwo muno, pamene ife tikutenga ndi kupereka nkhani yathu. Ife tikhazikitsa izi, mmawa uno, pa seweru. Ndipo ine, nthawi zambiri, kuno masiku angapo apitawo ine. . .

⁵³ M’bale ndi Mlongo Wood anali ndi ine, ine ndikukhulupirira, kumtunda uko pa msonkhano womaliza, ndipo ndinali kuyankhula pa Kadzutsa wa a Christian Business Men. Ndipo ndinapereka seweru laling’ono la Zakeyu mu . . . mu mtengo wa mkuyu, ndipo, pamene Yesu anabwera pamenepo, ndipo momwe iye anatengera chitini cha zinyalala, inu mukudziwa (ndipo ndinapanga izo ngati seweru), ndipo anakwera mu mtengo, kuti amuwone Yesu; mwamuna wamalonda atakhala mu mtengo, inu mukudziwa, akubisala kwa Yesu. Ndipo Yesu sankadziwa kumene iye anali, monga ngati, inu mukudziwa. Ndiyeno iye anati, “Oh, iwo amandiuza ine Mwamuna ameneyo amadziwa zinthu ndipo akhoza kuneneratu zinthu, ndipo amadziwa kumene nsomba inali ndi khobidi. Ine sindikuzikhulupirira zimenezo.” Ndipo Yesu anayenda kufika pansu pa mtengowo. Ndipo anati, “Oh, Iye sangandiwone ine, ine ndakhala mmwamba mu mtengo.”

54 Yesu anayima ndipo anayang'ana mmwamba, ndipo anati, "Zakeyu, tsika pansi." Samangodziwa kokha kuti iye anali mmwamba mmenemo, koma Iye ankadziwa yemwe iye anali.

55 Chotero ine ndikuganiza sewero pang'ono nthawizina limathandiza anthu okalamba, anyamata akale ndi atsikana, chimodzimodzi monga aang'ono.

56 Chotero tsopano inu mukhoza kundifunsa ine, izi zikatha, "M'bale Branham, inu mumazipeza kuti nkhani izi za anthu awa ndi maina?" Ena a iwo, ndathandizidwa ndi mzanga wabwino, M'bale Booth-Clibborn. Ndipo yina, ndi Josephus, wa zambari yakale wamkulu. Ndiponso mabukhu a mbiri yakale amene ine ndawerenga, a chochitika ichi, ndi zina zotero. Ndipo umo ndi mmene ine ndimapezera nkhani kuchokera ku zimene ife titapereke mu sewero mmawa uno, kwa ichi.

57 Ine ndikuwawona aang'ono athu akutuluka tsopano, ndipo ku nkhani iyi mmawa uno imene ife titaipereke. Tsopano anyamata inu ndi atsikana, ngati inu mungathe, ochuluka amene angafune, bwerani kutsogolo komwe kuno. Ife tiri ndi mipando yopanda anthu faivi kapena sikisi. Ngati mungafune kubwera komwe kuno, ife tikhala okondwa kukhala nanu. Iwo akungobwera mu nthawi ku sewero laling'ono pano.

58 Ndipo tsopano umo ndi mmene ine ndimapezera nkhani, momwe ine ndimapezera izo. Winawake akhoza kuzungulira ndikuti, "Chabwino, ine sindinawerengepo gawo limenelo mu Baibulo." Koma, ngati iwe sunatero, mbiriyakale inazitenga izo, inu mwaona. Chotero izo zonse ndi nkhani yomweyo, kungoti iyo inaperekedwa mu a—a—a mmawonekedwe a sewero pang'ono.

59 Ndipo, chotero, ndi zimenezotu! Ndi zimenezotu! Ameneyo ndi mng'ono wako? Oh, iye ndithudi akuwoneka ngati iwe! Ndipo iye ndi mnyamata wabwino. Iwe ukhoza kungowona kuti iye ali. Chabwino.

60 Tsopano inu mukufuna kubwera kuno ndi kudzakhala kuno? Pali atsikana aang'ono awiri, kapena atsikana aang'ono atatu. Mai, izo ndi zabwino ndi zokoma! Tsopano ine ndikufuna. . . Nkhani yaying'ono iyi mmawa uno ndi ya atsikana ndi anyamata. Missus Collins, ine ndikukhulupirira ndi iwe pamene, ndi mlongo wamng'ono winayo; iwe ukufuna kupita kumeneko, wokonedwa, ndi kukakhala pansi. Eya, ndikukhulupirira pali malo pano, ngati dona anga—angasunthe bukhu lake la mthumba. Ndipo—ndiyeno *apa* pali mipando ingapo apa.

61 Ndikuwafuna anyamata achichepere onse awa ndi atsikana kutsogolo kuno, kuti ndiyankhule nawo iwo. Apa, kuno ife tiri ndi mipando apa. Ife tikuwona kuti inu mukutenga mipando ina. Inde, bwana. Ina ya iyo itithandiza ife komwe kuno. Chotero, ife tikufuna ichi chikhale kwa anyamata awa ndi atsikana. Oh, mai! Kodi izo si zabwino? Tsopano ndizo. . . Ine ndikukhulupirira inu

mukuyenera kukhala ndi ingapo yowonjezera, M'bale Neville, ine ndikuwona angapo akubwera kuno. Ndipo tsopano izo ndizabwino basi!

⁶² Ndi amayi angati ali pano? Kwezani dzanja lanu. Oh, izo ndi zopambana! Tsopano, izo ndi zabwino ndi zokoma basi.

⁶³ Tsopano ngati atsikana aang'ono inu kumbuyoko mukufuna kubwera kuno, kazibwerani kuno, ngati inu ndinu aakulu mokwanira kukhala motalikana ndi amayi. Ndipo amayi akufuna kukubweretsani inu kuno, chabwino, awuzeni iwo kuti abwere. Izo ndi za amayi, nawonso. Chabwino, tsopano.

⁶⁴ Ine ndikukuuzani inu, ana, ife tangowerenga ndime. Kodi inu nonse mungakonde kuyibwereza iyo ndi ine? Kodi inu nonse mungakonde kubwereza ndime iyi ndi ine? Tsopano, iyo ikupezeka mu Mateyu Woyera, mutu wa 16 ndi ndime ya 25, chimene ife titi tiyankhulepo. Tsopano aang'ono awa... Mnyamata wamng'ono aliyense ndi mtsikana, mmawa uno, mubwereze iyi ndi ine tsopano: [Anyamata ndi atsikana akubwereza momutsanzira M'bale Branham—Mkonzi]. Nenani, “Mateyu Woyera, mutu wa 16, ndime ya 25.” Tsopano mubwereze ndi ine: “Pakuti aliyense amene adzasunga moyo wake adzawutaya iwo; ndipo aliyense amene adzataya moyo wake chifukwa cha Ine adzawupulumutsa iwo.” Adzawupulumutsa iwo. Tiyeni tinene izo kenanso: “Aliyense amene adzataye moyo wake chifukwa cha Ine adzawupulumutsa iwo.” Zopambana!

⁶⁵ Tsopano, anyamata ndi atsikana, inu mukudziwa chiyani? Pali zinthu zambiri mdziko zimene ziri zamtengo wapatali. Ndipo chimodzi cha zinthu zimenezo ndi, inu muli nacho lero, ndi solo imene ili mkati mwa thupi limenelo. Ndipo icho ndi chinthu chamtengo wapatali mdziko, kwa inu. Nkulondola uko, amayi? Nenani, “Ameni.” [Amayi akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chinthu chamtengo wapatali chimene inu muli nacho ndi solo yanu. Ndipo tsopano ngati inu musunga solo yanu, ndiye inu mudzayitaya iyo. Ndipo ngati inu mutaya solo yanu, ndiye inu mudzaipulumutsa iyo; ngati mudzatayire solo yanu kwa Yesu, mwaona. Mwa kuyankhula kwina, ngati inu mukhulupirira pa Yesu, mumadzakhala wophunzira Wake. Ndiyeno ngati muwupereka moyo wanu kwa Yesu pamene inu mudakali achichepere monga chonchi, ndiyeno inu mudza... Iye adzawupulumutsa iwo kukhala Moyo wosatha. Koma ngati inu—ngati inu mukufuna kuwusunga iwo, inu mudzawutaya iwo; eya, inu mudzawutaya. Inu mukufuna kumachita ngati atsikana ena awa ndi anyamata kozungulira kuno, ndi kumapita kunja ndi kumakachita momwe iwo amachitira, ndiye inu mu—inu mu—inu mudzawutaya iwo. Koma ngati mukufuna kupereka moyo wanu kwa Yesu, ndiye mudzawupulumutsa iwo kwa Muyaya ndi kwanthawizonse.

⁶⁶ Tsopano, inu muzikumbukira zimenezo tsopano, kuti ndi chinthu chamtengo wapatali mu dziko lonse, ndi solo yanu yaying'ono. Ndipo ngati inu mudzaisunga iyo, mudzayitaya iyo; ngati mungayipereke iyo kwa Yesu, inu mudzaipulumutsa iyo. Kodi munganene izo ndi ine? Ngati... [Anyamata ndi atsikana akubwereza momutsanzira M'bale Branham—Mkonzi]. Nenani, “Ngati ndingayisunge iyo, ine ndidzaitaya iyo; ndipo ngati ndingaipereke iyo kwa Yesu, ndidzaipulumutsa iyo.” Ndi zimenezotu! Tsopano inu mwamvetsa izo. Kodi sichoncho... .

⁶⁷ Amayi onse amene akuganiza kuti izo zinali bwino, nenani, “Ameni.” [Amayi akuti, “Ameni!”—Mkonzi]. Oh, zabwino zimenezo! Izo nzabwino.

⁶⁸ Tsopano, inu mwaona, pali chinthu chimodzi chimene inu mungachite. Tsopano, inu kazipitirirani. Ngati iwo akufuna kuti azichita monga izo, ndi kukhala ndi zofuna zawo za mdziko... Ngati anyamata ndi atsikana akufuna azipita kunja kumeneko ndi kumakachita zinthu, ndi kumakanena nkhani ndi kumakanena zinthu zimene ziri zolakwika, ndi—ndi kumanama ndi kuba, ndi—ndi kumakachita zinthu zoyipa, ndi kumakopera kusukulu, ndi zinthu, kumapitirira; iwo adzaitaya. Iwo adzaitaya iyo. Koma ngati inu mudzaipereka iyo kwa Yesu, iwo sadzachita izo, ndiyeno iyo idzapulumutsa izo. Izo ndi zimene inu mukufuna kuchita. Sichoncho izo?

⁶⁹ Tsopano ife tiyamba mu nkhani yathu yaying'ono. Tsopano, amenewo ndi maziko athu, tsopano inu mukumbukire zimenezo. Tsopano tiyeni tiyambe nkhani yathu yaying'ono. Tsopano, kwa anthu aakulu, ndi kwa a—abambo ndi amayi, inu mumvetsere, nanunso, tsopano; inu, makamaka inu amayi ndi abambo. Tsopano mungo... ndipo ife tikuyamba. Inu mumakonda nkhani zazing'ono? Sichoncho inu? Oh, ine ndimangozikonda izo! Makamaka tsopano... Inu mumawerenga nkhani zambiri zomwe sizowona. Koma nkhani iyi ndi yoona, mwamtheradi Choonadi, Mawu aliwone a iyo. Iyo ili mu Baibulo la Mulungu, chotero iyo ikuyenera kukhala Choonadi, mwaona, chifukwa Iwo ndi Mawu a Mulungu. Mawu a Mulungu ndi Choonadi.

⁷⁰ “Tsopano, inu mukudziwa,” anati, “Ine ndatopa kwambiri. Ine—ndine—ine ndatopa mokwanira kuti ndife.”

⁷¹ “Chabwino,” anati, “bwanji osapita mmwamba ndi kukagona? Ukagone pa bedi, pa mpando kumeneko, ndi kukagona.”

⁷² Iye anati, “Koma, oh, ine ndatopa kwambiri.” Iye anati, “Oh, wokonedwa, ngati iwe ukanawona zimene ndawona lero! Oh, ine... ine, chiyani... ine sindikufuna nkomwe chakudya chamadzulo chirichonse! Oh, izo ndizowopsya, chimene ndinachiwona lero!”

Anati, “Chabwino, iwe unawona chiyani?”

⁷³ Anati, “Chabwino, ine sindingakuuze iwe, pamaso pa ana, oh, izo ndizowopsya kwambiri! Mai, izo zinali zoyipa!”

“Chabwino, ndi chiyani chimene iwe unachiwona?”

⁷⁴ “Chabwino, ine ndikupita mmwamba ndipo ndikagona kanthawi pang’ono basi, ndiyeno—ndiyeno tikamaliza chakudya chamadzulo pamene tagonetsa ana onse, ndiye ine ndidzakuuzwa iwe chimene chachitika lero.”

“Chabwino,” iye anatero.

⁷⁵ Ndipo mmwamba iye anapita. Iye anakagona. “Oh, wotopa kwambiri! Oh, mai!” Inu mukudziwa momwe abambo amakhalira akatopa, basi akatopa kwenikweni!

⁷⁶ Ndipo patapita kanthawi, mtsikana wa maso owala, iye anayamba kuthamanga thamanga pansi, ndi kumayankhula mofuula pang’ono. Anati, “Shi-shi-shi, shi-shi-shi, usachite zimenezo. Uwadzutsa adadi. Ndipo, oh, iwo atopa kwambiri mpaka iwo—iwo amafuna kufa. Iwo samafuna konse kukhala moyo. Ndipo ngati abambo afika potopa choncho, chabwino, ife tiwalole iwo agone pang’ono. Musawadzutse iwo.” Ndipo Miriamu wamng’ono, iye akupita ndi kukakhala pansi, kuti akhale chete kwenikweni.

⁷⁷ Ndipo patadutsa kanthawi iye anakonza chakudya chamadzulo, chotero iye akupita mmwamba ndipo iye—iye akumuyitana iye, “Amram?”

⁷⁸ Ndipo iye anati, “Inde, Jochebed, kuno. Ine ndikubwera kumeneko.” Chotero iwo anatsika masitepe, inu mukudziwa, ndipo iwo anali ndi chakudya chamadzulo chabwino.

⁷⁹ Chotero iwo atadya chakudya chamadzulo, ndipo wamng’ono—mnyamata wamng’ono ndi mtsikana wamng’ono onse atadya chakudya chamadzulo chawo chonse, bwanji, iwo. . . amayi anawapititsa anthuwo ndipo anakawayika iwo pa bedi.

⁸⁰ Ndipo kenako anakalowa mchipinda, iye ndi mwamuna wake, ndipo iwo anakhala pansi. Anati, “Chabwino, tsopano, chinali chiyani chomwe unawona lero, Amram, chimene chakupangitsa iwe wo—wosokonezeka kwambiri usikuuno, kuti mpaka iwe sumafuna kukhala moyo?”

⁸¹ “Oh,” iye anati, “wokonededwa, ine—ine sindikukhoza basi kumvetsa zimenezo.” Iye anati, “Ine ndinawona. . . Chabwino, ife timaziwona izo tsiku lililonse, koma lero linali lapadera.” Anati, “Oh, ine—ine ndinawona chinthu chowopsya chimene ndinachiwonapo.” Anati, “Anyamata athu osauka, ena a iwo osapitirira usinkhu wa zaka thwelofu, akukoka ngolo yayikulu yakale imeneyo, ndi zingwe pakhosi pawo monga *choncho*. Ndipo ana osauka amenewo anakoka mpaka sakanakokanso, akukwera mtunda waukulu umenewo, miyala yaikulu imeneyo kumbuyo uko, ndipo iwo analephera kuti azipitirira. Ndipo

patapita kanthawi ngoloyo inayamba kupanga phokoso ndi kumayenda pang'onopang'ono kwenikweni, ndipo patapita kanthawi iyo inadzaima. Kumusi pa msewu kunadzabwera mwamuna, oh, iye anali wamisala! Iye anafuula, 'Nchifukwa chiyani inu mukuyimitsa ngoloyi?' 'Wham!' ndi zikwapu zazikulu za njoka zakale, ndipo akuwakwapula ku nsana, ndipo magari akuthamanga ku nsana kwawo, ndipo akuyenderera monga *choncho*. Ndipo ana aang'ono osauka amenewo anangowira chingwe ichi ndipo akulira." Anati, "Oh, Jochebed! Iye tingachite chiyani, amayi?" Anati, "Ife ndi anthu a Mulungu. Mulungu anatidalitsa ife. Ndife ana a Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo. Ndipo nchifukwa chiyani kuti ife tizikhala akapolo kumusi kuno kwa zinthu izi? Oh, ndi zowopsya momwe anyamata amenewo amalirira. Oh, ndipo ine ndinapemphera ndi kupemphera ndi kupemphera, Jochebed, ndipo izo zikuwoneka ngati Mulungu sakundimva ine nkomwe. Ine ndinapemphera ndi kupemphera, ndipo Iye akuwoneka ngati Iye wapereka khutu logontha, Iye sakundimva ine nkomwe. Iye akuwoneka ngati Iye sakusamala nkomwe."

⁸² "Tsopano," iye anati, "taona, Amram, izo sizikumveka ngati iweyo. Iwe ndi bambo weniweni, ndipo iwe . . . Izo sizikumveka ngati iweyo, chifukwa iwe nthawizonse umatirimbikitsa ife, kumatiuza ife kuti tizikhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu."

⁸³ "Oh, koma, wokonededwa, pamene ine ndikupemphera mochuluka, ndipo komabe Mulungu omasandimva ine, ndipo nkumawoneka ngati izo zikuyipirayipira nthawizonse. Pamene ndikupemphera mochuluka, pamene zikuyipirayipira."

⁸⁴ Koma, anyamata ndi atsikana, kodi Mulungu amamva pemphero? [Anyamata ndi atsikana akuti, "Inde."—Mkonzi]. Iye amamva pemphero. Kodi Mulungu amayankha pemphero? ["Inde."] Eya. Kodi Iye amayankha mwachangu? Osati nthawi zonse. Iye amatero? Ayi. Nthawizina Iye amatipangitsa ife kudikirira. Nkulondola uko? ["Inde."] Koma, Mulungu amayankha pemphero, amatero Iye? Ndipo basi chifukwa chakuti chirichonse chalakwika, chimenecho si chizindikiro chakuti ife tisiye kupemphera. Ife tizingopempherabe, mulimonse, ife sititero? Uko nkulondola. Tsopano, inu mwayankha bwino. Mulungu amayankha pemphero. Tiyeni tonse tinene izo pamodzi. "Mulungu amayankha pemphero." Inde. Ziribe kanthu zimene zikuchitika, Iye amayankha, mulimonse. Chabwino.

"Chabwino, kodi inu mupita kukapemphera kenanso?"

⁸⁵ "Inde." Ndipo abambo anali ndi chipinda chapadera kumtunda mmwamba kumene ankapita kukapemphera. Chotero iwo anapita kumeneko usiku umenewo, iwo akugwada pansu pambali, iwo anati . . . Tsopano iye anati, "Jochebed, tsopano kazipitirirani ndipo mupite muzikagona, ndipo iwe

ndi ana. Chifukwa, usandivutitse ine, ine ndikukapemphera mwinamwake usiku wonse usikuuno.”

⁸⁶ Chotero iye akugwada pamawondo ake, ndipo iye akupemphera ndipo akupemphera. Ine ndikumuwona iye akukweza mmwamba manja ake, ndipo akuti, “O Mulungu wa Abrahamu, Isaki, ndi wa Yakobo, mukumbukire lonjezo Lanu kwa anthu Anu! Apa ife tiri kumusi kuno mu Igupto, ndipo tiri mu ukapolo. Ndipo, oh, akuluakulu athu ankhanza a—akutipangitsa ife kupanga zinthu, ndi kumatimanya ife, ndipo anthu athu osauka a—akuvulidwa maliseche, ndipo akutikwapula ife ndi zikwapu. Ndipo ndife anthu Anu. O Mulungu, ndithudi Inu mumva pemphero! Ndithudi Inu muyankha pemphero! Ndipo ine ndikupemphera ndi kupemphera ndi kupemphera, ndipo Inu mukuwoneka ngati Inu simukundiyanika nkomwe ine. Koma, Mulungu, ine ndimakhulupirira kuti Inu ndinu Mulungu, ndipo Inu potsiriza mudzandiyankha pemphero.” Ndipo iye anapitirira kupemphera monga choncho, pafupifupi usiku wonse.

⁸⁷ Ndipo mmawa wotsatira, pafupifupi firii kapena foro koloko, iye akubwera kutsika masitepe aang’ono. Ndipo iye akuyang’ana kumeneko, ndipo pamenepo panali mkazi wake wamng’ono wokonedwa, Jochebed wamng’ono. Iye anali pamenepo pa bedi akugona. Ndipo Aroni wamng’ono ndi Miriamu wamng’ono anali atayikidwa kale pabedi, chotero iwo anali mtulo mmene iwo akanathera, ndipo akugona kumeneko. Chabwino. Iye akunena kwa iye. . . Iye anati, “Nthawi yatha, ndipo iwe ukungo. . .”

⁸⁸ “Eya, ine ndapemphera usiku wonse.” Maso ake anali atadetsedwa ndi misonzi, chifukwa iye amawalirira anthuwo.

⁸⁹ Ndipo iye anati, “Ona, Amram, iwe usamapite molimba pa izo.”

⁹⁰ “Tsopano,” iye anati, “tamvetsera, wokonedwa. Izo nzabwino. Koma tsopano taona, iwe uli ndi ana awiri oti uwalere apa. Ndipo cholemetsacho ndi changa. Ngati winawake sawapempherera anthu athu osauka, chitawachitikire iwo ndi chiyani? Chitachitike ndi chiyani ngati winawake samawaganizira anthuwo pa mtima? Winawake akuyenera kupemphera.”

“Chabwino,” iye akuti, “Amram, cholemetsa chonsecho si chako.”

⁹¹ “Chabwino, izo zikuwoneka chomwecho. Ndipo mulimonse, ine ndizipemphera, mulimonse, nthawi zonse!”

⁹² Anapita ku ntchito tsiku limenelo. Ndipo tsiku lililonse iye amabwera ndi kumapita, ndipo kuvutika kwakale komwe kuja. Ndipo iye anali ndi ntchito yovuta. Iye ankayenera ku. . . Iwo ankatsanulira matope mu zikombole zazikulu, ndipo

iyе ankayenera kumayima pamenepo pafupi ndi ng'anjo yayikulu imeneyo. Pamene iwo ayitsegula iyo, oh, mai, iyo imatsala pang'ono kusenda chikopa chake, kutentha koyipa kumeneko! Iye anakankhira njerwa zimenezo mmenemo ndi kumaziwotcha izo, nkumazitulutsa izo; kuti akamangire misewu yaikulu, ndi nyumba zazitali zazikulu, kwa milungu yamafano ndi chirichonse. Ndipo mwamuna weniweni Wachikhristu yuu kumusi uko akugwira ntchito monga choncho, kwa mdani. Koma iye anali kapolo, iye anali mu ukapolo. Iye ankayenera kuti achite zimenezo.

⁹³ Usiku uliwonse iye akabwera kunyumba, iye amapemphera. Ndipo amakwera masitepe kenanso, ndi kukapemphera ndi kukapemphera ndi kukapemphera, ndipo nkutsika pansi. Sizimasintha; zimakhala zikuipiraipira.

⁹⁴ Ndipo tsiku lina ali ku ntchito iye anamva mphekesera. Anati, “Ndi chiyani chimenecho? Ndi chiyani chimenecho? Ndiuzeni ine!” Winawake ananong'onezana ndi mzake. Patapita kanthawi, tsiku lisanathe, izo zinaliponseponse mdziko lonse, chimene chimati chichitike.

⁹⁵ Chinali chiyani icho? Gulu linali loti likumana usiku umenewo. Mfumu Farao yokalamba, mfumu yakale yankhanza yokalamba inali yoti iyitane anthu ake onse pamodzi, ndi kukakhala ndi msonkhano wina waukulu. Chotero iwo anali ndi msonkhano waukulu uwu kumusi kumeneko.

⁹⁶ Chotero usiku umenewo iye analowa, oh, iye anali yense wokhumudwa. Iye akulowa, ndipo mkazi wake akuti, “Amram, wokondedwa,” iye anakumana naye iye pakhomo ndipo anamupsyopsyona iye, ndipo anati, “ndakonzachakudya chamadzulo chabwino ndi chotentha. Koma,” anati, “wokondedwa, iwe ukuwoneka wotuwa. Vuto ndi chiyani?”

⁹⁷ Anati, “Oh, Jochebed, ngati iwe ukanangodziwa chimene chikuchitika! Oh, izo zayipa kuposa kale!”

“Chiyani?”

⁹⁸ “Shi-shi, sindinganene izo, ana ali pafupi. Udikire mpaka chakudya chamadzulo, ndipo ine ndikuuza iwe za izo.”

“Chabwino.”

⁹⁹ Chotero, iye anali atakonzachakudya chamadzulo. Ndipo anadya, ndipo anawatenga ana ndi kukawagonetsa iwo.

¹⁰⁰ Chotero, iwo anakalowa. Iye anati, “Jochebed, ine ndikufuna ndikuuze iwe chinachake.” Anati, “Chimodzi cha zinthu zowopsya chikuchitika.”

“Chiyani?”

¹⁰¹ Anati, “Iwo akhala ndi msonkhano wina lero, usikuuno. Ndipo pamene iwo atero, iwo ayika cholemetsa china pa anthu ife.”

¹⁰² Chotero, ndiye, tiyeni tipite uko ku nyumba ya amfumu. Mfumu Farao akuwabweretsa iwo onse kunjya uko, ndipo anati, “Chabwino, akuluakulu nonsenu! Vuto ndi chiyani ndi inu amene muli pano? Ine ndikupereka kulamula kwanga pano! Anthu awa akuchulukana nthawi zonse! Vuto ndi chiyani? Kodi ife sitingaletse izi?” Anati, “Tsiku lina padzabwera gulu lina la ankhondo kuno. Ndipo adani athu onsewa, kuchokera ku Goshen mpaka uko, a Israeli awa, adzadzijowinitsa okha ndi gulu la ankhondo ili, ndipo iwo adzatisonjitsa ife. Ndipo chuma chathu chachikulu chidzagwetsedwa pansu, ufumu wathu waukulu udzawonongedwa. Iwo adzatitenga ife. Vuto ndi chiyani ndi inu? Yankhulani, winawake! Kodi inu simukudziwa chinachake choti muyankhule?” Oh, iye anali woyipidwa, ndipo woyipidwa kwambiri. Akuluakulu onse, akunjajemera.

Mmodzi wa iwo anadzuka, ndipo anati, “Mukhale ndi moyo wautali Mfumu Farao.”

“Chabwino, nena chimene iwe utanene!”

¹⁰³ Anati, “Mukhale ndi moyo wautali mfumu. Wolemekezeka inu, bwana,” iye anati, “Ine ndingakonde kuti inu muyike zolemetsa zochulukana pa anthuwa.”

¹⁰⁴ “Iwe chigaza-chakufa! Munayika kale zolemetsa zambiri pa anthuwo, komabe iwo akuchulukana. Bwanji, iwe, ngati amenewo ndi maganizo onse amene uli nawo, ungowasunga iwo kwa iwemwini!” Oh, iye anali wovuta.

¹⁰⁵ Patapita kanthawi mmodzi anadzuka, kumwetulira kwakukulu pa nkhope yake, ngati mdierekezi. Ndipo iye anati, “Mukhale ndi moyo wautali Mfumu Farao.” Anati, “Ine ndiri nalo lingaliro.”

Anati, “Chabwino, yankhula! Usayime pamenepo monga choncho!”

¹⁰⁶ Iye anati, “Ine ndikuuzani inu chimene ife tingachite.” Anati, “Inu mukudziwa, anthu awa akuchulukana mofulumira.”

¹⁰⁷ “Inde, uko nkulondola!” Anati, “Ena a iwo, ena a anthu awo ali ndi ana ochulukana mpaka kufika fortini, nthawizina iwo amakhala ndi ana twente. Ndipo anthu athu alibe mwina mmodzi.” Anati, “Iwo akuchulukana mofulumira, iwo akungodzadza dziko lonse.”

¹⁰⁸ Mwaona, Mulungu anali akuchita chinachake. Mwaona, Mulungu nthawizonse amakokera ubweya pamaso pa mdierekezi, inu mwaona. Mukuona? Iye amadziwa chimene Iye akuchita. Mukuona? Ndipo akazi onsewa akungokhala ndi ana ambirimwina.

¹⁰⁹ “Bwanji,” iye anati, “mukhale ndi moyo wautali mfumu. Chabwino, ine ndikuuzani inu chiyani. Nthawi iliyonse mkazi akabereka mwana wamwamuna. . . Mupite kunjya mdzikoli kuno ndipo mukapeze amayi ena amene sana. . . amene si amayi.

Inu mwaona, amayi amene sanakhalepo ndi ana, amayi amene sakufuna ana ndipo samawakonda ana, afiti akale a mphuno-zazitali. Mwaona, mphuno zazitali, zabwinoko! Zala zakale zazitali nkhope zopentedwa, ndipo mukawatenge iwo. Iwo samadziwa chimene chikondi cha amayi chiriri. Chotero ndiye pamene mwana wamwamuna abadwa, bwanji, muziwalola iwo azipita ndi kukamutenga mwana wamwamuna uyo, ndi kubwera naye nkudzammenyetsa mutu wake ku khoma, kumuponyeranso iye mnyumba kwa amake monga choncho. Kukamuponyera iye pansu mu chitsime chachikulu. Oh, zabwinoko kuposa zimenezo, kumutulutsa iye ndi kukamumanga manja ake ndi mapazi, ndi kukamuponyera iye uko, ndi kukanenepetsera ng'ona. Umo ndi mmene mungathanirane nazo izo. Mukatero iwo sachulukana kwambiri, chifukwa sikudzakhala amuna otsalira; titapha ana onse aamuna.”

¹¹⁰ “Oh,” Farao akuti, “izo nzabwino! Limenelo ndi lingaliro labwino!” Mukuona chimene mdierekezi ali? Iye ndi mthakati, sichoncho iye? Anati, “Chotero icho ndicho chinthu choti tichite! Pitani mukatenge. . .Iwe uli. . .Tsopano, pokhala kuti unali ndi lingaliro, ine ndingokupanga iwe ukhale woyang'anira wa zimenezo. Iwe upite kunja ndipo ukatenge akazi onse okalamba amene iwe ukuwadziwa, amene—amene sanakhalepo amayi, ndipo samakonda ana. Ndipo iwo a. . .” Iwo. . .

¹¹¹ Inu mwaona, izo zimatengera mayi kuti amukonde mwana. Inu mukukumbukira momwe amayi anakukonderani inu? Chabwino, tsopano mwaona, amayi amakonda ana aang'ono.

¹¹² Koma iwo ankayenera kumutenga winawake amene—amene iwo sana. . .amene analibe ana, sankafuna ana, basi—basi—basi amayi okalamba ankhanza kwenikweni. Ndipo anati, “Muwapange iwo akhale apolisi. Ndipo pamene inu muwapanga iwo apolisi, ndi kuwalamulira iwo kuti apite mnyumba iliyonse imene iwo akuyifuna, ndi kukamutenga mwana aliyense ndi kukamenyetsa mutu wake kukhoma, ndi kukampereka iye kwa ng'ona kuti amudye. Mwana wamng'ono aliyense!” Oh, ndi zankhanza bwanji! Ndiye inu mukudziwa zimene iwo anachita?

“Chabwino, izo ndizabwino!”

¹¹³ Kenako tsiku lotsatira pamene Amram anali kumusi kumeneko akugwira ntchito, iye anamva kuti nkhani imeneyo yavomerezedwa.

¹¹⁴ Oh, iye akupita kwawo. Iye anati, “Oh, Jochebed! Oh, wokonedwa, ndilole ine ndikuuze iwe chinachake. Iwe ukudziwa chimene lamulo limenelo linali, limene laperekedwa? Kutu azipha makanda aamuna onse.” Ndipo iye anamuza iye. Anati, “Oh, ine ndikulephera kuzipirira izo.” Iye anakweranso mmwamba, kuti akapemphere. Usiku umenewo iye anapemphera kuposa kale lonse.

115 Kodi ife tikuyenera tizingopempherabe? Oh, zipempheranibe! Nkulondola uko? Muzingopitirira kumapemphera, ziribe kanthu chimene chikuchitika. Muzingopempherabe!

116 Tsopano, ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, iye anapemphera usiku wonse, “O Mulungu, tichitireni chifundo! Tithandizeni, Mulungu! Ife tikupemphera kuti Inu mutithandize ife mwa njira inayake.” Anabwereranso pansi, pafupifupi masana.

117 Tsiku ndi tsiku, ndipo, oh, kufuula kotani kuzungulira dzikolo! Tsiku lililonse iwo amakhoza kuwamva amayi akufuula, mokwera ndi motsika mmisewu. Iwo ankatenga makanda awo kuchokera mmanja mwawo, aang’ono awo, makanda aamuna owoneka bwino. Afiti akale amenewo ankapita mmenemo ndipo, amatenga mapazi awo aang’ono, ndi kukawamenyetsa iwo kukhoma ndi kuwapha iwo, ndi kukawaponyera iwo kwa ang’ona. Mayi womvetsa chisoni ankagwada pa mawondo ake, ndipo ankalira, “Oh, musamutenge mwana wanga! Musamutenge mwana wanga!” Ndipo, oh, ndi nthawi yotani yomwe iwo anali nayo!

118 Inu mukudziwa momwe amayi amakondera khanda laling’ono, ndi momwe amawamenyera iwo pa chibwano. Kumbukirani momwe amayi ankakutengerani inu ndi—ndi kukusambitsani inu, ndi kukupsyopsyonani inu, ndi—ndi—ndipo ankanena mmene inu munaliri okongola. Ndi momwe iwo ankaugonetserani inu usiku. Ndipo, oh, ngati—ngati inu munga...khomo laling’ono likatseguka, kampemera kakang’ono kakamadutsapo, chinachake monga choncho, oh, mai, iye ankathamanga mofulumira ndi kukatseka chitsekocho, kumufunditsa mwanayo, ndipo, inu mukudziwa, iye ankamutenga iye. Iye anakakukondani inu. Mukuona? Iye anakakukondani inu. Oh, iye anakakakonda kanthu kakang’ono kosaukako kamene Mulungu anampatsa iye, kamene kanali kopanda thandizo ndipo sikanakadzithandiza kokha, chotero iye anakukonda mwana ameneyo. Ndipo iye ankaugowapsyopsyona ana ake ndi kumasewera nawo iwo, chifukwa iye anali mayi weniweni. Mukuona?

119 Koma akazi akale awa amene amapha ana, iwo sankadziwa chimene chikondi cha amayi chinali. Iwo sanali amayi. Zonse zimene iwo ankaganiza, iwo amangokhala ndi nthawi yopambana mmalingaliro awo, zinthu za mdziko, chotero iwo ankapita ndi kukapha ana amenewo. Inu ndi ana kwambiri kuti mudziwe, koma izo zikupitirirabe. Uko nkulondola. Tsopano akuluakulu inu mukudziwa chimene ine ndikukamba. Uko nkulondola, zochuluka za izo! “Oh,” inu mukuti, “ine sindingachite...” Koma nkhani zotaya mimba ndi chinthu chomwe chomwecho. Chabwino, koma inu mwaona iwo

samadziwa chimene chikondi cha amayi chiri. Tsopano inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza pamene ine ndikuti “amayeni enieni!” Uko nkulondola. Palibe kusiyana; mdierekezi yemweyo! Chotero pamenepo, ndiye, iwo... Tangoganizani za masauzande kuchulukitsa masauzande kuchulukitsa masauzande, chaka chirichonse, moyipa mmene izo zinaliri mu Igupto, kapena kuposerapo.

¹²⁰ Ndipo kumeneko, ndiye, iwo amabwera, iwo analibe chikondi cha amayi, chotero iwo ankawatenga ana aang’ono amenewo ndi kumawapha iwo. Oh, izo zinkayipirayipira ndi kumayipira. Ndipo tsiku lina panadzabwera mphekesera ina, iwo akhala ndi msonkhano wina.

¹²¹ Farao anayitana nduna zake zonse pamodzi, iwo, onse a iwo pamodzi, iwo analowa mmenemo: anati, “Chabwino, iwo akuchulukanabe! Ife tichita chiyani za izo tsopano?”

¹²² Mnyamata yemwe uja wotheathyalika wokalamba, wa nkhope ya mdierekezi, anadzuka. Iye anati, “Mukhale ndi moyo wautali Mfumu Farao. Ine ndiri ndi lingaliro. Taonani, inu muli nawo anthuwo akugwira ntchito. Inu muwapangitse iwo aziwumba njerwa, zochuluka chomwechi tsiku lililonse, muwapange iwo kuti aziwumba izo ndi mapesi. Inu mwapha a—ana aang’ono ndi zinthu, koma iwo akuchulukanabe. Chinthu chimene inu mukuyenera kuchita, ndi kuwapangitsa amayi azigwira ntchito, nawonso. Ngati inu mungawapangitse azimayi kumagwira ntchito, ndiye iwo sa...” Tsopano, amenewo si malo a mkazi. Ayi. Chotero iwo anati, “Koma inu muwapangitse akazi azigwira ntchito, ndipo mukawayike iwo kunjira uko, ndipo muwalole iwo aziwumba njerwa, nawonso. Ndiyeno iwo azikhala otopa kwambiri pamene iwo akuweluka, iwo—iwo samawaphikira chakudya chamadzulo azimuna awo, iwo samakhala amayi abwino, mwaona. Ndipo chotero ngati iwo azipita kukagwira ntchito ndi kumapitirira monga choncho, chotero iwo—iwo samakwanitsa kuchita zimenezo. Chotero, inu muwapangitse iwo azigwira ntchito, nawonso.”

¹²³ “Izo nzabwino! Mai, ndiwe bambo wanzeru.” Chotero iye akukawayika akazi onse kuti azigwira ntchito.

¹²⁴ Ndipo apa pakubwera Amram wokalamba wosauka, anabwera usiku umenewo, anati, “Oh, Jochebed, ine sindikudziwa chimene ife titi tichite. Tsopano iwo akuwapangitsa amayi onse kuti azigwira ntchito. Ine—ine ndikukuuza iwe, oh, ine sindikudziwa basi choti ndichite! Ndife—ndife—ndife basi... Ndife akapolo, ndipo ife tikuyipira ndi kuyipira. I—ine ndikuneneratu izi: ngati Mulungu angatichitire konse ife chirichonse, icho chidzakhala ife tonse titafa.”

¹²⁵ Tsopano, Mulungu samadikira monga choncho, Iye amatero? Ayi. Mulungu amangotiyang'anira ife nthawizina, Iye samatero? Chabwino.

¹²⁶ Chotero ndiye usiku umenewo, iye anati, "ine ndikukwera mmwamba ndipo ndikukapemphera ngati kuti sindinapempherepo!"

¹²⁷ Tsopano, umo ndi mmene tiyenera kupempherera, sichoncho izo? Kupemphera ngati sunayambe wapempherapo, kutanthauza kwenikweni zimenezo! Mwaona, ngati inu mungapite ndi kukati, "Ambuye, mumudalitse *Wakuti ndi wakuti ndi wakuti*," Mulungu sama—samakhala ndi chidwi kwa izo. Koma pamene inu mutanthauza kwenikweni zimenezo! Pamene anyamata aang'ono inu ndi atsikana mupemphera, muzitanthauza zimenezo! Kodi inu mumachita zimenezo ku sukulu? Inu mumatero—inu mumamupempha Mulungu kuti akuthandizeni inu ku sukulu? Pamene—pamene inu mukumapita ku sukulu, ndipo inu simukukhoza bwino, inu muzipita ndi kukati, "Mulungu, ine—ine ndikufuna kuti Inu mundithandize ine."

¹²⁸ Kodi inu mumapemphera? Ndi anyamata angati ndi atsikana amene amapemphera? Tiyeni tiwone manja anu. Oh, izo nzabwino. Tsopano, izo ndi zabwino. Kodi inu muli ndi malo obisika amene mumapita kukapemphera, kumene amayi ndi abambo samakuwonani nkomwe? Kodi inu mumapemphera monga choncho? Inu—inu simupemphera monga choncho? Mukhale ndi malo aang'ono, muzizemberako ndi kukapemphera, ndi kukanena pemphero lanu laling'ono. Inu muzilina ilo usiku uliwonse musanagone? Pamene mwadzuka mmawa, ndi chinthu? Oh, izo nzabwino. Ndi anyamata ndi atsikana ena angati (kwezani mmwamba dzanja lanu) amene amapemphera? Paliponse mchipindachi. Oh, kodi izo sizabwino? Chabwino, tsopano, izo nzabwino. Izo zimawonetsera kuti inu muli ndi amayi enieni ndi abambo amene amakuphunzitsani inu kuchita zinthu izi. Tsopano, tsopano pamene inu mwasowa kwenikweni, inu bola muzipemphera moonamtima. Sichoncho inu?

¹²⁹ Chotero, Amram wamng'ono, anakwera mmwamba. Oh, mai! Iye sanafune chakudya chamadzulo. Iye anati, "Izo ndizoyipa kwambiri. Mai!"

"Oh," iye anati, "inu mukuyenera mudyemgonero, adadi."

"Sindingachite basi zimenezo, Jochebed. Ine sindingachite basi zimenezo. Ine—ine . . ."

¹³⁰ "Oh," anati, "koma iwe ukuwonda, ndipo iwe uli ndi manjenje, ndipo watuwa nkhope yako. Iwe ukusanza chakudya chako, ndi zinthu."

131 “Oh, ine sindikudziwa choti ndichite! Koma,” iye anati, “wokonedwa, ngati winawake sawaganizira anthuwo, ngati winawake samawapempherera anthuwo, ife tichita chiyani? Ife tikhala tikumayipirabe. Ndithudi, nthawi zina, Mulungu adzamva!”

132 Inde, uko nkulondola. Uko nkulondola. Mulungu adzamva. Inu muzitsimikiza za izo ndi kungokhala pamenepo!

133 Oh, nthawi iyi iye akupita mmwamba mosiyana. Pamene iye akupita mmwamba nthawi iyi, iye akukagwada pansi, akuyika manja ake mmwamba mlengalenga, akufuula, “Mulungu, ine ndikuyankhula ndi Inu tsopano!” Amen. Akuyamba kugwira ntchito! “Mulungu, Inu muli ndi makutu, ndipo Inu mukhoza kumva. Inu muli ndi maso, ndipo Inu mukhoza kuwona. Inu mumakumbukira; Inu mumawadziwa Mawu Anu. Inu mukudziwa lonjezo Lanu. Ine ndikukuchonderani Inu, Mulungu, muyang’ane pansi kuno, Ndinu Mulungu wa Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo, kuti anthu Anu ali mmavuto, ndipo iwo akufa. Muchite chinachake kwa ife, Mulungu! Ife tikuyenera kukhala ndi Inu pakamodzi! Ife tikungoyenera kukhala ndi Inu, kapena ife tifa. Ife tikuyenera kukhala ndi Inu. Ife tikungoyenera kutero, ngati ife tingakhale moyo.” Pamenepo ndi pamene inu mumapemphera kwenikweni. Oh, iye anapemphera!

134 Inu mukudziwa, nthawizina anthu pamene iwo akupemphera, iwo amatopa. Kodi sichoncho, amayi ndi abambo? Oh, amatopa kwambiri! M’bale Branham nthawizina amatopa kwambiri mpaka ine ndimatsala pang’ono kukomoka pamene ndipita kukapemphera nthawi yaitali; ndimangokomoka, kumapita wopanda kudya, ndi zinthu, kwa masiku; ndi kumapemphera ndi kupemphera ndi kupemphera, ndi kulalikira. Ndipo ine ndimangofika pamalo amene ine ndingakomoke, pafupifupi. Ndipo nthawizina anthu amapita mwanjira imeneyo. Imeneyo si nthawi yogonja. Zipitiriribibe! Mulungu adzayankha! [M’bale Branham akugogoda pa guwa katatu—Mkonzi]. Inde, bwana. Zigwiritsitsanibe! Inde, bwana.

135 Chotero iye akukwera mmwamba pang’ono, masitepe akale opanga phokoso. Ndipo ine ndikumuwona Jochebed akubwera, ndipo akuti, “Oh, Amram, usatero. Wokonedwa, ine—ine ndikukhulupirira. . .”

136 “Tsopano, Jochebed, taona, iwe uli bwino, wokonedwa. . .” Iye anali mayi wokongola, wowoneka bwino wamng’ono. Ndipo iye anamupsyopsyona iye pa tsaya, inu mukudziwa, ndipo anamuisita iye monga *choncho*. Anati, “Tsopano, amayi, inu mubwerere ndipo mukamugonetse Aroni ndi—ndi Miriamu wamng’ono. Ndipo ine ndikupita mmwamba kukapemphera. Ndipo tsopano, ngati ungandimve ine ndikulira, iwe usati ubwere mmwamba.”

137 “Chabwino, koma, Amram, iwe ukuchita chiyani, wokonedwa? Iwe wangotsala pang’ono kufa.”

138 “Inde, koma ine—ine ndiri ndi kupsyinjika chifukwa cha anthuwa pa mtima panga. Ine ndikuyenera kuti ndichite chinachake za izo. Ine ndikuyenera ndikhale pa mawondo anga. Ndipo chotero anthu onse...” Iye anati, “Lero, lero lokha, kumusi ku phiri la njerwa, ine ndinali kumusi kumeneko, anakhala akunena, ‘Chabwino, ndithudi, Mulungu atimva!’ Ndipo bambo mmodzi wokalamba wamkulu anadzabwera, anadzayika manja ake mchiuno mwake, ndipo anati, ‘Kodi Iye adzakumva liti? Kodi Iye adzakumva liti?’ Mukuona momwe anthu akuyipirayipira? Iwo akumatsutsana ndi Mulungu, chifukwa iwo amapemphera ndi kupemphera ndi kupemphera, ndipo palibe chimachitika. Ndipo uyu amapemphera ndi kupemphera ndi kupemphera, ndipo palibe chinachitika. Ndipo ansembe onse akuti, ‘Masiku a zozizwitsa anapita, ndipo chinthu chokhacho chimene ife tingachite ndi kungotsikira kwa olamulira akale awa amene amapembedza chikunja, kapena milungu yachikunja, ndi zina zotero. Ndipo kodi ife tingachite chiyani?’” Koma iye anati, “Koma ine ndimakhulupirira mwa Yehova! Ameni! Ine ndikukhulupirira Iye amayankhabe pemphero!”

139 Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni!”—Mkonzi]. Inu mukukhulupirira izo? Ameni! Nonse a inu amene mukukhulupirira zimenezo, nenani, “Ameni.” [“Ameni.”] Amayankhabe pemphero! Chabwino.

140 Thupi lofooka laling’ono lakale, linataya thanzi lochuluka. Akukwera masitepe ophokosera iye akupita, akupita kumeneko ndipo akukagwada pansu. Iye anati, “O Yehova!” Oh, iye anapemphera ngati kuti sanayambe wapempherapo! Iye anati, “Yehova, taonani kuno! Inu ndi Mulungu weniweni. Ife tikukhulupirira kuti Inu muli nawo makutu. Ife tikukhulupirira Inu muli nawo maso. Ndipo Inu mumadziwa zinthu zonse. Ndipo ife tikukhulupirira Inu ndi Mulungu wa Ahebri, ndipo ndife anthu a lonjezo. Ife tikukhulupirira Inu mumasunga Mawu Anu.” Anati, “Awoneni achikunja awa kunja kuno, momwe iwo akutengera ntchito yathu yotchipa, ndi kumamanga misewu yayikulu ndi mafano, ndi chirichonse. Inu, Yehova, kodi Inu mungakhale Kumwamba ndi kuwalola achikunja azilamulira pa Inu? Ine sindikukhulupirira kuti Inu mungachite zimenezo.” Ameni!

141 Ine sindikukhulupirirabe kuti Iye adzachita zimenezo! Ameni! Pamene mdierেকেzi abwera, Mulungu akadali Mulungu! Kulondola! Iye sangalole adierekezi awa kuti achite zimenezo. Ine ndikukhulupirira izo, lero, kuti pamene zamakono ndi zamkutu, ndi zovunda zonsezi zikuchitika; komabe, Mulungu amalamulirabe ndipo Iye akadali Mulungu! Kulondola!

Chimene ife tikusowa ndi winawake ngati Amram, amene angakhale ndi cholemera pa mtima pawo, amene angakhale pamenepo ndi kuzipempherera izo, kufikira Miyamba itatseguka uko, Mulungu nkutsika pansi ndipo nkuyankha pemphero. Amen.

¹⁴² “Tsopano onani apa,” iye anati, “Mulungu, kodi Inu mukuwalola achikunja azinyoza anthu Anu monga chonchi? Masabata ndi miyezi ndi zaka zadutsa. Ife tikupemphera mosalekeza, ndi misonzi, koma... [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. O Mulungu, kodi Inu mungavomereze chinthu choterocho?”

¹⁴³ Ine ndikudabwa lero, kuti pamene mahandirede a makanda akuponyedwa mu mitsinje ndi zithaphwi, ndipo osaloledwa kuti akhale moyo, ndipo nkhani zochotsa mimba ndi chirichonse zikuchitidwa; O Yehova, kodi Inu mungaloleze zinthu zoterozo kuti zizipitirira? [M’bale Branham wagoda paguwa ka sikisi—Mkonzi]. Lero, pamene kachasu ndi mowa, ndi moyo wausiku, ndi chirichonse, zikufuula mokweza. Ndipo ngakhale guwa lafooka kwambiri mpaka iwo akuwopa kuti anene chirichonse cha izo. Yehova, kodi Inu mungavomereze zamkhutu zoterozo kuti zizipitirira? Iye adzayankha tsiku lina. Oh, mkwiyo Wake ndi wowopsya iwo ukadzabwera. Inde, bwana. Akazi kumapita kunja ndi kumakapanga diso la mwana wawo poyika ndudu, kuti azikaponyeramo phulusa, ndi chirichonse. Ndipo anthu kumatengera makanda awo kunja kumalo omwera mowa, atsikana aang’ono ndi anyamata atakhala pamenepo, usinkhu wa zaka sikisi kapena eyiti, kumamwa, ndi zinthu monga choncho. Ndipo dziko kumavomereza izo, ndi, “Izo ziri bwino.” Oh, mai! Mukuganiza kuti Yehova samawona zimenezo? Pamene, iwo akuwaseka anthu amene akulondola kwenikweni ndi Mulungu. Zinthu zonzezi zikuchitika, kumawaseka. Gwiritsitsani, musingogwiritsitsa! Yehova adzayankha. Musadandaule. Chabwino.

¹⁴⁴ Ife tipite chitsogolo pang’ono. Ife tikumupeza iye kumeneko akupemphera. Ndipo iye watopa kwambiri, iye wangozigoneka pansi. Iye akungopemphera mpaka wangogwera pansi. Iye sangapitirirenso, ndiye anagona pang’ono. Iye anadzuka. “Chavuta ndi chiyani? Onani pozungulira kuno! Kuwala kumeneko kukuchokera kuti? Oh, taonani, atayima pamenepo pakona.” Pamenepo panayima Mngelo, lupanga Lake liri pamenepo pambali Yake. Oh, iye anayang’ananso, ndipo anapukuta maso ake. Iye anadzuka pa mawondo ake, iye anati, “Ambuye, oh, oh, chiyani—Inu mungafune chiyani kwa ine?”

¹⁴⁵ Iye anati, “Amram, Ine ndi Mngelo wa Mulungu. Ine ndatumidwa kuchokera Kumwamba, kuti ndidzakuuze iwe kuti Mulungu wamva pemphero lako. Ndipo ine ndabwera kudzakuza iwe kuti Iye atumiza muwomboli.

Iye akukumbukira malonjezo Ake onse.” Ine ndikumuwona Mngelo tsopano; muwoneni Iye, Iye akusolola lupanga lake. Iye akulozetsa ilo kumpoto. Amram akuyang’ana. Iye anati, “Kumene lupanga ili likuloza kuli dziko lolonjezedwa. Ndipo Ine ndinamulonjeza Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo, abambo ako, kuti anthu inu mudzatenga dziko limenelo. Ndipo Ine ndamva kubuula kwa anthu, ndamva kulira kwa ana, ndipo Ine ndatsika pansi. Ndipo Ine ndikufuna kuti iwe udziwe kuti iwe usewera gawo lalikulu mu ichi, Amram, chifukwa iwe unali wokhulupirika mu pemphero. Iwe unali wokhulupirika mnyumba yako. Ndipo pafupifupi nthawi iyi chaka chamawa, Jochebed, mkazi wako wamng’ono wokondedwa, adzakhala ndi mwana wamwamuna. Ndipo mwana wamwamuna ameneyo adzakhala muomboli.” Ulemelero!

¹⁴⁶ Iye anati, “Oh, inde. Inde. Oh, inde. Inde. Oh, Iye ndi wokongola kwambiri.” Iye anayang’ana, ndipo Mngelo anayamba kukwera mmwamba. Zinangowoneka ngati kuti miyamba yonse inatseguka, ndipo Iye anatuluka mchipindamo. Iye anadikira kanthawi pang’ono. Iye anati, “Oh, ine sikuti ndabalalika.”

¹⁴⁷ Kutsika masitepe iye anapita, mofulumira kwenikweni, ndipo anati, “Jochebed! Jochebed, fulumira!”

Anati, “Inde, vuto ndi chiyani, wokondedwa?”

¹⁴⁸ Anati, “Dzuka!” Ndipo kuwala kwa mwezi kukuwalira pa zenera, anali. . . Iye ankawoneka mokongola. Ndipo iye anati, “Ine ndangomuwona kumene Mngelo wa Mulungu, ndipo Iye wandiuza ine zinthu zonsezi.”

“Oh, kodi Iye amawoneka motani?” anatero mayiyo. “Iye amawoneka motani?”

¹⁴⁹ Anati, “Oh, Iye anali wokongola. Iye anali atavala mwinjiro wowala. Maso ake amanyezimira. Ndipo Iye anali ndi lupanga mdzanja Lake, ndipo Iye analozetsa ilo kumpoto.” Mbali yake ndi kumeneko, inu mukudziwa, dziko lolonjezedwa liri ku Igupto; kumtunda njira imeneyo, Palestina. Iye anati, “Iye analoza kumpoto. Ndipo Iye ananena kuti ife tikhala ndi mwana pafupifupi nthawi ino chaka cha mawa, ndipo mwana uyu adzabwera ndipo adzakhala mgonjetsi, ndipo adzawombola anthu Ake. Oh, alaluya, Jochebed!”

¹⁵⁰ Ndipo iye anazindikira kuti iye anayera. Nkhope yake, maso ake anali akuyang’ana, maso ake aakulu akuyang’ana. “Jochebed, vuto ndi chiyani?”

“Oh, Amram! Ayi, ayi, ayi! Ife tikhala ndi mwana wamwamuna?”

“Inde.”

151 “Oh, iwe. . . Izo sizingatheke. Iwe ukudziwa chiyani? Oh, ngati iwe ukanapanda kukhala ndi masomphenya awa. Iwe ukudziwa chiyani, Farao, iye akupha ana onse.”

152 “Inde. Koma, iwe ukudziwa, ngati Mulungu angatipatse ife mwana uyu, Mulungu adzamsamalira mwanayo. Ameni! Mulungu analonjeza. Mulungu adzamusamalira iye.”

153 Chabwino, tsiku lotsatira iye akupita kukagwira ntchito. Ndipo anzake onse kumeneko, iwo akumuwona Amram. Mmalo mobwera, inu mukudziwa, pokhala wowerama ndi wofooka, anadzutsa mapewa ake, anati, “Ndipatsireni njerwa zina zowonjezera. Bwera, tiye tizipita!”

“Chavuta ndi chiyani?”

“Ulemelero kwa Mulungu! Mulungu ayankha pemphero.”
Oh, ayi. . .

154 Inu mukudziwa, izo zimakupangitsa iwe kumverera bwino pamene upeza yankho. Kodi ife sitikudziwa zimenezo, abambo ndi amayi, pamene Mulungu apereka yankho? Iwe sumasowa kuwona masomphenya. Umangodziwa kuti yankho liri pamene, ndizo zonse. Ndizo zonse, kungodziwa kuti yankho liri pamene.

155 Tsopano, mvetserani mwatcheru tsopano, ndikufuna inu mumvetsere, chimene chinachitika. Tsopano inu mukudziwa, patapita kanthawi, anati, “Chabwino, Amram, vuto ndi chiyani ndi iwe?”

156 “Mulungu ayankha pemphero! Mulungu ayankha pemphero!”

“Chabwino, Iye ayankha pemphero motani?”

“Izo sizikupanga kusiyana kulikonse.”

157 Bambo wina wokalamba anabwera, ndipo anati, “Tsopano iwe ukuganiza kuti Iye adzayankha liti?”

158 “Chabwino, ine sindikuuza iwe, chifukwa iwe ndi wosakhulupirira, mulimonse. Ndipatseni njerwa zina zowonjezera.” Anaziponyera izo mmenemo monga *choncho*. . .? . . . Sindikusamala; inu simumasowa kuwauza osakhulupirira zinthu zonse, sichoncho inu? Sizipanga kusiyana kulikonse. Ayi, bwana. Ndithudi ayi. “Ndipatsireni njerwa zina zowonjezera. Aleluya! Ayankha pemphero!” Umo ndi mmene umamverera pamene ukudziwa chimene chitachitike. Si choncho izo? Inde, bwana.

“Chabwino, Iye achita izo motani?”

159 “Iwe sukudziwa, mulimonse, chotero uzingopitiriza kumaperekera njerwazo.” Anaziika zonse mmenemo, anaziika njerwa zonse zakale mmenemo.

160 Usiku umenewo iye anapita kwawo, anati, “Oh, Jochebed, taganiza za zimenezo, ife tikhala ndi mwana! Oh, iye adzakhala

muwomboli! Mulungu adzamutumiza iye. Oh, izo zidzakhala zopambana.”

“Oh, koma inenso . . .”

¹⁶¹ “Oh, usiye kudandaula! Usiye kudandaula! Mai! Mulungu ali—Mulungu ali mbali yomvetsera tsopano. Mulungu ali nawo makutu; Mulungu akhoza kumva. Mulungu ali ndi manja; Iye akhoza kuwombola.” Chotero, oh, iye anali ndi chikhulupiriro chochuluka.

¹⁶² Inu mukudziwa, pamene inu mwapemphera, inu mukapeza yankho, inu mumapeza kwenikweni chikhulupiriro chochuluka pamenepo. Oh! Kodi inu munayamba mwapemphererapo chinachake, ndipo inu nkudziwa kuti Mulungu akuchitirani inu icho? Kodi atsikana aang’ono inu mumachita zimenezo, ndi anyamata inu? Eya. Ndithudi. Pamenepo ndi pamene Iye . . . Pamenepo ndi pamene inu mumadziwa kuti izo zichitika. Chabwino.

¹⁶³ Chaka chonse kudutsa. Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, apa pakubwera Amram akuchokera kuntchito tsiku lina. Ndipo chinachitika ndi chiyani? Mwana wokongola kwambiri, oh, iye anali wokonededwa wamng’ono, pafupifupi wotalika *chonchi*. Ndipo chotero iye anamunyamula iye, nkumupereka iye kwa Amram. Ndipo iye akumupsyopyona iye, inu mukudziwa. Iye amamukonda iye, mwaona. Ndipo amayi anali atamuyangata iye. Oh, ndi chuma chotani! Iye anati, “Oh, ine ndiri ndi mantha kwambiri, ngakhale, inu mukudziwa. Mwana uyu, iye ndi kanthu kokoma kakang’ono.”

¹⁶⁴ Ndipo inu mukudziwa chiyani? Baibulo linati ameneyo anali mwana wokongola kwambiri amene anayamba wabadwapo. Tsopano ine ndikudziwa amayi sagwirizana ndi ine pa izo. Uh-huh. Iwo amaganiza . . . Amayi anu amaganiza kuti inu munalu mwana wokongola kwambiri. Sichoncho inu? Eya. Iwo ali ndi ufulu woganiza zimenezo. Koma Baibulo linati uyu anali mwana wowoneka bwino. Oh, iye anali ngale. Mulungu anali ataika manja Ake pa iye, inu mukudziwa. Chotero, oh, iye anali chinthu chaching’ono kungongola! Iye amagona pamenepo, ndipo iye—iye amakhoza kungomwetulira pang’ono, wopanda mano.

¹⁶⁵ Inu munalibe mchimwene wamng’ono ndi iwo, amene ankachita zimenezo, pamene iye analibe—analibe mano, amangomwetulira monga *choncho*?

Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, “Wah!”

“Oh, mai, kalanga! Psyii! Ine ndikudziwa, tiyeni tikangomubisa iye.”

“Chavuta ndi chiyani? Iwe ukuchita chiyani?”

¹⁶⁶ “Umutengere iye kupansi. Iwe ukudziwa chimene lamulo liri. Mwaona, ngati afiti amphuno zazitali amenewo angabwere kuno, iwo adzamutenga mwana wathu ndi kumupha iye. Uko

nkulondola. Ife sitingamulole iye kuti azilira.” Chotero, oh, iye ankafuna wina—ankafuna kadzutsa wina kapena mgonero. Chotero amayi akumutengera iye pakona, akukamuyamwitsa iye, inu mukudziwa. Ndipo chotero iye anali wabwino bwino nthawi imeneyo.

¹⁶⁷ Chotero mausiku angapo zitatha zimenezo, iwo anali kusewera ndi iye, ndipo, “Wah!” Kutali iye anapita kenanso, inu mukudziwa, anayamba kukalira. Iye anapita mofulumira kwenikweni, ndipo anakamubisa—anakamubisa iye mwachangu monga choncho. Ndipo kupansi, pansi penipeni mmbuyo, mu khoma, Amram anali atakonza malo aang’ono kumene akanakamubisa mwanayo.

¹⁶⁸ Ndiyeno chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo anamva chinachake mmwamba chikupita... [M’bale Branham akugogoda paguwa—Mkonzi]. *Psyii!* Wapita! Aliyense anamwazikira ku malo amodzi, anati, “Ndi amenewo. Ndi afiti okalamba aja amenewo, azala-zazitali zakale, zikhadabo zopenta!” Ndi afiti okalambawo... Anayang’ana pansi pamenepo, ndipo anayang’ana panja pa zenera, anati, “Eya, ndi amenewo. Iwo ayima kumeneko.”

[M’bale Branham akugogoda pa guwa—Mkonzi].
“Tsegulani!”

¹⁶⁹ Amram wokalamba anatuluka, anadzatsegula chitseko, anati, “Mukufuna chiyani?”

¹⁷⁰ Anati, “Inu muli ndi mwana muno, ndipo ife tikudziwa zimenezo. Ndipo ife tikudzamutenga iye.”

“Ife tiribe mwana woti tikupatseni inu.” Iwo analibe.

¹⁷¹ “Ife tikulowa ndipo tidzayang’ana, mulimonse. Ife ndi apolisi achikazi. Mukuona mabaji athuwa?” Ndipo ndizo... Kodi izo sizoti mkazi akhale? Koma, “Ife ndi apolisi achikazi. Ife tatenga maufulu athu kuchokera kwa a ulamuliro!” Inu mukudziwa, ife tiri nawo iwo kuno tsopano. Ndipo chotero—chotero ndiye iwo akuyambapo, akulowa. Iwo akulowa ndipo akukatembenuza mpando, ndi kutsegula makabati onse, ndipo akuponyera chirichonse panja pansi, ndipo akutenga zovala zonse zapabedi ndi kuzikutumula izo. Ndi kupita mmwamba ndi kukapeza kumene abambo anali ndi malo obisika. Anayang’ana paliponse, koma iwo sanamupeze mwanayo.

¹⁷² Sanakhoze kumupeza mwanayo, chotero iwo anapita kwa mkaziyo kumeneko, wosauka—Jochebed wosauka atayima pamenepo, nkhope yake inali itayera. Iwo anapita, anati, “Yang’ana kuno! Ife tikudziwa kuti ndiwe—mayi. Ife tikukhoza kudziwa ndi momwe iwe ukuwonekera. Ife tikudziwa kuti iwe ndi mkazi woyamwitsa, ndipo tikudziwa kuti mwana ameneyo ali muno. Tibwereranso. Tidzamtenga iye!” Anatuluka pa

khomo nkumapita. Anamenyetsa chitseko, ndipo anatuluka panja nkumapita.

Iye anati, “Oh, oh, kodi ife tichite chiyani? Kodi ife tichite chiyani?”

¹⁷³ Chotero Amram anati, “Pemphera.” Kodi ndicho chinthu choti tichite? [Anyamata ndi atsikana akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Chinthu chake ndi chimenecho? “Pemphera! Tiyeni tipemphere.”

“Oh, oh, oh! Ine sindikudziwa choti—choti ndichite. Oh!”

¹⁷⁴ Chotero iye anati, “Tsopano, taonani, iwe ukhale chete, ndipo upite ukamuyamwitse mwanayo kenanso. Ine ndikupita mmwamba ndi kukapemphera.”

¹⁷⁵ Chotero iye akupita mmwamba ndipo akukapemphera. Iye anati, “Yehova, Inu muli nawo makutu. Yehova, Inu muli nawo maso. Yehova, Inu mukhoza kumva. Inu mukhoza kuyankha. Inu munatipatsa ife mwana uyu. Inu munatipatsa ife lonjezo Lanu. Ndipo Inu musunga lonjezo Lanu, ndipo Inu mumusunga mwana ameneyo. Ndipo ndine wotsimikizika!”

¹⁷⁶ Atatha kupemphera, atatopa kwenikweni, iye—iye anangogwa monga *chonchi* ndipo anagona. [M’bale Branham akutsanzira kuliza nkonono—Mkonzi]. Iye anali atatopa kwambiri! Atagwira ntchito tsiku lonse, ndi kupemphera usiku wonse. Iye anali atatopa. Ndiyeno kodi inu mukudziwa chimene chinachitika? Iye anapita kukagona, ndipo analota loto.

¹⁷⁷ Inu mukudziwa, Mulungu amayankhula mmaloto, nayenso, sichoncho Iye? Ndithudi, Iye amatero. Inde, Iye amatero. Iye akhoza. Mukuona? Ndipo Iye amayankhula mmaloto.

¹⁷⁸ Oh, pamene iye anadzuka, iye anati, [M’bale Branham akukhwatchitsa chala chake kamodzi—Mkonzi]. “Ndi zimenezotu! Ine ndimayenera kuganiza za izo. Izo ndi zimene ine ndikuyenera kuchita.” [M’bale Branham anagogoda paguwa kasanu.] “Ine basi sindinena kanthu ka izo.”

Akutsika pa masitepe iye akupita. Iye anati, “Jochebed!”

“Inde, wokonedwa? Oh, ine ndatopa kwambiri. Ine ndikukanika kugona.”

“Oh, pita ukagone. Pita ukagone. Izo zonse zatha.”

“Iwe ukudziwa bwanji?”

“Oh, ine ndikungodziwa. Ine ndangokhala ndi chidaliro!”

¹⁷⁹ Mmaloti bamboyo, usiku umenewo, apite mmwamba kuti akapemphere, iye anatsikira pansu mchipinda cha pansu. Iye anali wotanganidwa pansu kumeneko. Ine ndikudabwa zimene iye anali kuchita. Tiyeni tipite pansu ndipo tikamuwone iye. Ine ndikumuwona iye pansu kumeneko, akupita. . . [M’bale Branham akuyamba kung’ung’udza, ndi kumaponda pamene akutsanzira kumanga kwa chinachake—Mkonzi]. “Pha, pha,

pha.” [M’bale Branham akung’ung’udza.] Kutenga bango ili, ndi kuliyang’ana ilo, kulipinda ilo ndi kuwona ngati liri labwino. [M’bale Branham akung’ung’udza.] Aroni wamng’ono anatuluka panja tsiku limenelo, ndipo anasonkhanitsa lodzadza nkono, analiyika ilo pansu mchipinda chapansi, inu mukudziwa. [M’bale Branham akung’ung’udza.] “Mulungu amakusamalirani inu.” [M’bale Branham akung’ung’udza.] “Chipembedzo chakale, icho chonse chikuyenera kukhala choona!” [M’bale Branham akumenya chinachake.] Kuwamanga iwo pamenepe.

Iye anati, “Amram, vuto ndi chiyani ndi iwe?”

“Aleluya! Palibe, wokonededwa. Zipitirira.”

¹⁸⁰ [M’bale Branham akung’ung’udza.] “Ndi chipembedzo chakale.” [M’bale Branham akumenya kenanso.] “Ndi chipembedzo chakale.” Bweretsa ichi *apa*, inu mukudziwa. “Ndi chipembedzo chakale.” “Shhhhhhh,” akumata icho chonse. “Ndipo icho ndichabwino kwa ine! Ndipatseni ine chakale ichi. . .” Iye anali akuchita chinachake.

¹⁸¹ Inu mukudziwa, patadutsa sabata kapena awiri, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo ankadabwa chimene iye amapanga.

¹⁸² Chotero usiku wina pamene iwo onse anali atagona, iye anapita mmwamba ndipo anakabweretsako chinthu chaching’ono ichi, inu mukudziwa. Iye akuchinyamula icho monga *chonchi*. Ndipo akuchibweretsa icho. Iye akukwezera mmwamba chofunda pamene Jochebed mkazi wake akugona, ndipo akukachiyika icho pansu pa chofundacho. Ndipo Aroni wamng’ono ndi—ndi Miriamu wamng’ono anali atagona, inu mukudziwa; oh, iye anali kanthu kakang’ono kokoma, mtsikana wamng’ono ameneyo anali, ndipo chomwechonso anali Aroni wamng’ono. Chotero, iye akukachiika icho pansu pamenepe. Iye anati, “Jochebed, wokonededwa.”

¹⁸³ Iye anati, “Kodi iwe unali pansu kukapemphera nthawi ino ya usiku, Amram?”

Anati, “Ayi. Ine ndakhala ndiri mchipinda chapansi, kumuyamika Mulungu.”

Anati, “Iwe umachita chiyani?”

¹⁸⁴ Anati, “Ine ndikufuna ndikuuze iwe. Tsopano, iwe ukudziwa amfiti okalamba aja akubweranso.”

“Eya.”

¹⁸⁵ “Ndipo ine ndikufuna ndikuuze chimene ife titachite. Ife takhala naye mwanayo tsopano kwa miyezi itatu, ndipo ife tikuyenera kumuchotsapo iye.”

“Oh, Amram! Iwe ukufuna kuchita chiyani?”

“Ife tikuyenera kumuchotsa mwanayu.”

“Kumuchotsa mwanayu?”

“Eya.”

“Oh, iwe ndi wankhanza!”

“Ayi, ine sindine wankhanza. Ayi, ayi, ayi. Ine ndikudziwa chimene ndikuchita.”

¹⁸⁶ “Iwe ukutanthauza chiyani? Bwanji, iwe ukhala woyipa monga ngati Farao. Ukufuna kumuchotsa mwana wathu?”

“Eya, ukufuna kumuchotsa mwanayu.”

“Oh, ife sitingatero!”

¹⁸⁷ “Tsopano mvetserani. Ngati ife titi timusunge iye, ife tidzamutaya iye. Ndipo ngati ife titi timupereke iye kwa Iye Amene anampereka iye kwa ife, Iye adzampeza iye.” Nkulondola uko? “Tsopano, ngati iwe uti umusunge iye, ife tidzamutaya iye.”

“Iwe umutaya chotani iye?”

“Bwanji, amfiti okalamba aja abwera ndipo adzamutenga iye.”

¹⁸⁸ Ndipo taonani, ngati musunga solo imeneyo ndi kumapitirira ndi kumakhala monga dziko, inu mudzaitaya iyo. Amfiti aku gehena akukulondolani inu. Ndipo uko nkulondola. Kupusa konse uku kwa dziko lapansi ndi zinthu kunja uko, zikulondolani inu. Ngati inu muisunga iyo, inu mudzaitaya iwo; koma ngati muyibwezera iyo kwa Iye Amene anayipereka iyo kwa inu, inu mudzayipeza iyo ndipo mudzayisunga iyo. Ndi chiyani icho tsopano? Kuti tiyisunge iyo, ife titani? [Ana akuti, “Tiyitaye iyo.”—Mkonzi.] Tiyitaye iyo. Ngati ife tiyipereka iyo kwa Khristu, ife titani? Tiyisunga iyo. [“Tiyisunga iyo.”] Ameni! Izo nzabwino. Tsopano mukuyankha bwino.

¹⁸⁹ Tsopano iye anati, “Jochebed, ife timutaye iye ngati tingamusunge iye. Chotero ngati ife tingampereke iye—kumupereka iye kwa Iye Amene anampereka iye kwa ife, ndiye ife timusunga iye.”

¹⁹⁰ Tsopano inu muli ndi solo. Ndipo, abambo ndi amayi, inu chimodzimodzi. Koma ngati inu muyisunga iyo, inu mudzaitaya iyo. Uko nkulondola. Amfiti aku gehena adzayitenga iyo. Iwo onse akuyifuna iyo! Koma ngati inu mungayipereke iyo kwa Iye Amene anaipereka iyo kwa inu, inu mudzaisunga iyo mpaka ku Moyo wosatha. Aleluya! Ameni! Mundikhululukire ine, ana, ine—ndine wachikale basi mokwanira kuti ndifuule. Ngati inu muisunga iyo. . . Tiyeni tinene izo, tonse pamodzi: [Osonkhana akunena limodzi ndi M'bale Branham—Mkonzi]. “Ngati muisunga iyo, inu mudzaitaya iyo; ngati mungayipereke iyo kwa Iye Amene anapereka iyo kwa inu, inu mudzaisunga iyo.” Ameni. Kumbukirani tsopano, iperekeni iyo kwa Iye.

¹⁹¹ Tsopano tiyeni tiwone. Oh, iye akuyamba kulira. Iye anati, “Oh, iwe uchita naye chiyani iye?” iye anatero.

“Taonani apa, ine ndikufuna ndikuwonetse iwe chinachake.”

“Wayika chiyani pansi pa bedi yanga pamenepo?”

Anati, “Ndilole ine ndikuwonetse iwe.” Ndipo iye anachitulutsa icho.

“Oh, ndi dengu laling’ono la bango!”

¹⁹² Ndi ngalawa yaing’ono, imene iyo ili. Ilibe popalasila, iyo ilibe chogwira mphepo, ilibe mifuti pa iyo, ndipo komabe iyo ikukanyamula katundu wofunikira kwambiri amene anayamba wanyamulidwapo ndi ngalawa, mpaka nthawi imeneyo. Imvani izo! Iyo ilibe woyang’anira kapena ogwira ntchito. M’bale, ine ndikuidziwa Ngalawa ya wamkulu, monga choncho, nanenso!

¹⁹³ “Oh,” iye anati, “Am- . . . ndilole ine ndiyiwone iyo, Amram, ndilole ine ndiyiwone.” Iye akupita pamenepo.

¹⁹⁴ Anati, “Tayang’ana apa, ili ndi chivinikiro chaching’ono pa iyo. Mukuona?” Iye akunyamula chivinikirocho mmwamba.

Iye anati, “Psyii! Kununkha! Uh! Psyii! Mai!”

Anati, “Inde, iyo ikununkha.”

“Bwanji?”

¹⁹⁵ “Ndainathira iyo kudzadza ndi phula. Iyo yonse yamatidwa, paliponse.” Phula ndi tara, inu mukudziwa, chotero iwo anaiyika phula kuzungulira iyo. Icho ndi chimene iye ankawiritsa kumusi kumeneko, ndi kuthira izo pamwamba pa mabango awa. Iye anali atayimata iyo. Anati, “Waona, madzi sangalowe mkati mwake. Waona, iyo yamatidwa paliponse.” Ndipo anati, “Ndipo iwo sangalowe basi mkati mwake, madziwo sangathe. Ine ndayimata iyo.”

Anati, “Psyii! Ikununkha moyipa!”

¹⁹⁶ Ana inu mukudziwa chimene phula liri, pamene iwo akukonza msewu, “Oh, fungo loyipa limenelo!” Koma ilo—ilo—ilo—ilo limapangitsa a . . . Ilo—ilo limatseka ming’alu yonse pa msewu. Ndipo umo ndi momwe ili limachitira, ilo limawatsekera kunja madzi onse.

¹⁹⁷ Ndipo ndicho chimene pemphero limachita kwa wokhulupirira. Icho ndi chimene chimapangitsa tsiku ndi tsiku kuti dziko likutalikireni inu, ndi pamene inu mudzimata nokha pa maondo anu, ndikuti, “Ambuye Yesu!” Ndipo Magazi amabwera pansi, ndipo Iwo amadzakusindikizani inu kuti mdierekezi asakupezeni inu. Mukuona? Uko nkulondola. Mukuona? Chotero ndiye, oh, nthawi zambiri anthu amapita mozungulira ndipo amati izo ndi zowopsya, koma, izo sizipanga kusiyana kulikonse, izo zimakupangitsani inu kukhala otetezeka. Ndicho chinthu chenichenicho, kukhala wotetezeka. Kumati, “Inu ndi achikale,” koma, izo ziribe ntchito, izo zimakupangitsani inu kukhala otetezeka.

“Chabwino,” anati, “ife tipanga chiyani?”

198 “Chabwino,” anati, “Ndikuuza iwe chimene ife titi tichite. Ife timutenga mwanayo, ndipo ife tikhala ndi kulekana pang’ono. Ndipo timutenga mwanayo ndi kumuyika iye umu, ndi kukamuyika iye uko mu Mtsinje wa Nailo.”

199 “Oh! Ayi! Ayi! Ayi! Amram, iwe sungakamuyike mwana wathu uko mu mtsinje.”

200 “Inde! Inde! Ine ndikudziwa chimene ndikuchita.” Mwaona, iye anali atalota loto, iye ankadziwa choti achite. Mwaona, Mulungu anali atamulangiza iye. Iye ankadziwa choti achite. Iye anamanga ichi, ndipo iye anawona kuti unali mtundu womwewo wa chombo chimene chinamupulumutsa Nowa kumbuyo uko mu nthawi yake.

201 Chotero iye anati, “Ona apa, ine ndaboola bowo laling’ono pamwamba pa iyo, kuti iye azitha kupuma. Waona, iye azikhoza kupeza kuwala kwa dzuwa kudzera pamenepo.”

202 Ndipo inu mukudziwa, chombo mu Chipangano Chakale, kumbuyo uko, icho chinkapangidwa mwanjira yomweyo. Ndipo chinkakhala ndi bowo pamwamba pake, kuti mudzitha kuwona mkati, inu mwaona, ndi pamene iye ankayenera kumawonera mmwamba.

203 Chotero ndiye mwana wosauka uyu, wopanda dzina, analibe dzina nkomwe; wamng’ono, mwana wopanda dzina, ndipo komabe mwana wokongola kwambiri mdzikolo.

204 Usiku wotsatira, pamene iwo anabwera, ndipo iwo anadikirira mpaka pafupifupi firii koloko mmawa, ndipo kenako iwo...Iye akuyenda. Ndipo anali atamaliza kupemphera. Iye akupita, ndipo iye anati, “Tsopano tiye, Jochebed, dzuka!”

205 Ndipo chotero iwo anamudzutsa Aroni wamng’ono ndi Miriamu wamng’ono. Oh, iye anabwera ndipo anayika manja ake, iye anati, “Adadi!” Miriamu wamng’ono, iye anati, “Inu simumutenga mchimwene wathu wamng’ono, mwana, inu mutero, ndi kukamuyika iye mu Nailo kumene kuli ng’ona zakalezo?”

206 Ndipo iye anakokera tsitsi lake laling’onolo mmbuyo monga *choncho*. Ndipo ake...Iye anali ndi maso okongola, ndi tsitsi laling’ono lokongola. Ndipo chotero iye anamupsyopsyona iye pambali pa tsaya. Iye anati, “Wokondedwa, izo zikundipweteka ine, nanenso. Izo zikundipweteka ine, nanenso, koma ife tikuyenera kuchita ichi.”

207 Inu mwaona, atsikana aang’ono ndi anyamata, nthawizina ife timayenera kuchita zinthu zimene zimakhala ngati zotipweteka ife, koma timayenera kuchita zimenezo, mulimonse. Pamene atsikana ati, “Heyi, iwe unasutapo ndudu?”

Inu nkuti, “Ayi.”

208 “Chabwino, udzayese imodzi! Oh, ndine mzako, iwe ukudziwa. Eya, iwe udzayese izo.”

209 Koma iwe, izo zikhoza kukupweteka pang’ono, koma uziti, “Huh-uh. Ine sindikuifuna iyo.” Mukuona? Mukuona? “Ine sindikuifuna iyo.”

Akati, “Kodi iwe ubwera, tipite ku kanema ndi ine madzulo uno?”

210 “Ayi, ayi. Huh-uh. Ine sindimapita ku makanema.” Mukuona? Izo zikhoza kupweteka pang’ono. Mukuona?

211 “Oh, iwe ndi munthu wachikale wokalamba.” Iwe usakhulupirire zimenezo. Zikhoza kupweteka pang’ono pokha. Ungotembenuza mutu wako kuchoka kwa izo; icho ndi chinthu choyenera kuchichita, inu mwaona. Nthawizonse muzichita zimenezo, muzichita chinthu choyenera. Chabwino.

212 Ndipo tsopano pamene atsikana akuphunzira kuvina ndizala zakumapazi kwachikale kwakung’ono uku monga choncho, ndipo akufuna inu muchite zimenezo; inu mudziwauza iwo, “Ayi, ayi.” Inu musamachite izo, mwaona.

213 “Oh, chabwino, ndi zosangalatsa kwambiri.” Inu simukusamala kuti ndi zosangalatsa mochuluka bwanji. Inu mukufuna kumapanga zimene ziri zoyenera, mukatero nthawizonse muzipanga zimene ziri zoyenera. Tsopano, mungokumbukira zimenezo tsopano. Inu musayiwale izo, sichoncho inu?

214 Tsopano, tsopano kodi iwo anachita chiyani? Iwo anamutenga mwana wamng’ono pamene, ndipo anapita kumeneko. Ndipo Aroni wamng’ono anabwera, ndipo anati, “Adadi, inu muchita naye chiyani mwana wathu?”

215 Iye anati, “Aroni, khala apa pamwendo panga, wokonedwa.” Anati, “Tayang’ana, Aroni. Ngati ife tingamusunge mwanayu, ife tipanga chiyani?” [Osonkhana akuti, “Timutaya iye.”—Mkonzi]. “Timutaya iye. Koma ngati titamupereke mwanayu mmanja mwa Iye amene anamupereke iye kwa ife, ife tichita chiyani?” [“Tidzamusunga iye.”] “Ife tidzamusunga iye.” Kulondola kumeneko.

“Koma inu muchita motani izo, adadi?”

216 “Ine sindikudziwa. Ine sindikudziwa mmene izo ziti zichitikire, koma Mulungu achita zimenezo.” Mukuona?

217 Ndipo chotero ndiye iwo anakamuyika mwanayo mmenemo, ndipo chotero iye akupita. Ndipo apa iwo akupita tsopano, iwo akupita pa chitseko. Iwo akupita kumusi pa chitseko, iye akuyang’ana mbali *iyi* kumusi kwa msewu, mbali *iyi* kumusi kwa msewu. Kulibeko kulikonse, kulibe aliyense akubwera.

Anati, “Zibwera, Jochebed. Zibwera, Aroni. Bwera, zibwera, Miriamu. Tiyeni tizipita.”

218 Iwo akutenga chombo chaching’onocho ndipo akupita kumusi ku mbendera pa mtsinje. Oh, ndi nthawi yayitali kusanache. Ndipo apa akubwera Aroni wamng’ono, kumbuyo uko atamugwira Miriamu wamng’ono, mchimwene wamng’ono ndi mchemwali, iwo anali akulira. Ndipo Jochebed wamng’ono wosauka, akupita nawo, akuti, “psyi, psyi, psyi, psyi.”

“Shi-shi-shi-shi-shi! Iwo akuyang’ana ku msewu. Musamale. Shi! Musamale.” Akupita kumusi kwa msewu. “Shi-shi-shi! Musamale.” Atamunyamula mwanayo. Ndipo amayi anali atamunyamula mwanayo, ndipo—ndipo abambo anyamula chombo.

219 Iwo akupita kumusi ku mtsinje. Oh, iwo ndi mtsinje waukulu, wachiwiri kukula mu dziko lapansi, pafupifupi. Ndipo chotero, ndiye, mtsinje waukulu, ndiponso wothamanga, ndipo wodzadza ndi ng’ona zazikulu zakale ndi ng’adzi. Oh, izo zinali zonenepa. Psyii! Iwo anali atadzidyetsa izo zonse ana amenewo. Izo zinali zitangonenepa. Ndipo—ndipo iye akuti, Jochebed akuti kwa Amram, mwamuna wake, anati, “Oh, nanga bwanji ngati ng’adzi zitamugwira iye? Nanga bwanji ngati ng’ona kuno zitamugwira iye?”

220 Anati, “Usadandaule. Ngati izo ziika mphuno zawo pa phula limenero, izo zithawapo, mwaona. Ndi chifukwa icho chikununkha, mwaona. Iyo izimata mphuno zake,” anati, “iyo singanunkhize thupi la munthu, chotero iyo idzangothawapo. Phula limenero lizinunkha moyipa mpaka izo zithawa. Izo zikhala bwino. Iwe usadandaule.” Chotero iwo... Ndipo pamenepo anayika icho pansu, chombo chaching’onocho. Ndipo iye anati... “Tsopano iwe umuyamwitse mwanayo.”

221 Chotero amayi akumutenga mwanayo ndi kumuyamwitsa iye, ndipo iye akumuyamwitsa mwanayo mpaka atapeza kadzutsa wake, mmawa molawirira. Ndipo kenako iye [M’bale Branham akupanga phokoso lopsyopsyona—Mkonzi]. akumupsyopsyona iye. Ndipo anati, “Tsopano, Aroni, iwe ukhoza kumupsyopsyona iye.” Ndipo Aroni akumupsyopsyona iye. Ndiyeno akumupititsa iye kwa Miriamu, ndipo iye akumupsyopsyona iye. Ndipo amayi akumupsyopsyona iye, ndipo, “Oh,” iye anati, “Ine basi...”

222 “Tsopano, shi-shi-shi! Tsopano mvetserani, ife tikuyenera kukhala asirikali. Mukuona? Ife tikuyenera kukhala asirikali. Tsopano inu nonse mukufuna kumupsyopsyona iye kenanso?” Onse a iwo akumupsyopsyona iye, mzungulira, kenanso. Kenako iwo akumuyika iye mmenemo.

223 Ndipo amayi anapanga bulangete laling’ono, ndi kudzaliyika pa iye, ndi pilo wamng’ono. Iye anamuyika iye

pamenepo. Iye anati, “Mwana wanga wokonedwa, Mulungu akudalitse iwe.”

“Shi-shi-shi! Tsopano, Mulungu amusamalira iye. Inu musadandaule.”

²²⁴ Anatsekera chivinikiro chaching’onocho. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, abambo akuyamba kuchotsa chikhotho chawo, kuvula malaya awo. Apa iye akupita, akukalowa mmadziwo.

²²⁵ Kodi inu mukuganiza kuti Kumwamba kukuchitika chiyani, nthawi imeneyi? Aleluya! Inu mukudziwa, pamene zinthu zikuchitika pansi pano, kumakhala chinachake chikuchitika kumwamba Kumeneko, aponso. Ameni! Ine ndikukhoza kumuwona Mulungu akudzuka pa Mpando Wake wachifumu, akuyenda, ndikuti, “Gabrielo! Gabrielo! Iwe uli kuti?”

Gabrielo akuti, “Ine ndiri pano, Ambuye.”

²²⁶ “Bwera kuno! Ndikuwonetsa iwe chinachake!” Anati, “Angelo nonsenu bwerani mudzazungulire kuno, miniti, Ine ndikufuna ndikuwonetseni inu chinachake. Ine ndiri ndi anthu amene amandikhulupirira Ine. Inde, ndiri ndi anthu amene amandidalira Ine. Bwerani kuno, miniti! Izo ndizabwino kwa Angelo nonsenu, mudzayang’ane izi. Penyani!”

“Ziri kuti zimenezo?”

“Pansi pomwe uko. Penyani.”

“Eya, eya. Eya, ine ndikuwona izo.”

²²⁷ “Taonani pansi kumeneko. Mukuona mmbali mwa ilo—ilo—ntcheza limenelo uko, mbendera zimenezo ndi zinthu?”

“Eya.”

“Taonani kumeneko!”

“Ndi chiyani chimenecho?”

²²⁸ “Pali munthu wakweza manja ake mmwamba mlengalenga, ali pa mawondo ake, akuitanira pa Ine. Pali mayi akulira, ndi ana awiri aang’ono akulira. Iwo akundidalira Ine mpaka kumapeto. Gabrielo, iwe ukukumbukira pamene unapitako? Iwe ukumukumbukira bambo ameneyo?”

²²⁹ “Inde, ine ndinakumana naye mchipinda usiku umenewo ndipo ndinayankhulana naye. Uh-huh.”

²³⁰ “Iye akundidalirabe Ine. Ine ndiri nawo anthu amene amandikhulupirira Ine! Ine ndiri ndi anthu amene amandikhulupirira Ine mpaka kumapeto!” [M’bale Branham akugoda pa guwa kasikisi—Mkonzi]. “Ukumuwona iye? Tamuyang’ane iye.”

“Inde, oh, uko si kulimba mtima!”

²³¹ Abambowo akulowa mmadzi, akuyamba kukankha ngalawa yaing’onoyo.

Ine ndikumumva Iye akuti, “Gabriele!”

“Inde, Ambuye?”

232 “Itanira Angelo teni sauzande apite pamalopo. Uwalamulire iwo kuti ayambe kuguba nthawi yomweyo. Itana makamu a Kumwamba atuluke. Uwatumize iwo onse mokwera ndi motsika, mbali mwa zotchinga za Kumwamba, ndipo ukawayike iwo onse mokwera ndi kutsika Nailo. Ine ndikulamula kuti palibe ng’ona itagwire katundu ameneyo! Palibe chitamugwire iye! Usalole ngakhale chidutswa cha nkhu chibwere pafupi ndi iye.” Aleluya!

233 Gabriele anati, “Izo zichitidwa.” Mai! Iye anawomba lipenga! Angelo teni sauzande anabwera ndi zida!

“Woyendetsa. Inu mukhala pati, Ambuye?”

234 “Ine ndikakhala kumapeto kwinako.” Iye nthawizonse amakhala mbali yolandirira. “Ine ndikadikirira mbali inayo. Ine ndiri ndi cholinga. Pamene anthu andidalira Ine, Ine ndimakhala ndi chinachake, cholinga; izo zimadzawayendera bwino iwowo.” Chabwino, Iye akupita kumusi ku mbali inayo.

235 Ndikumuwona Mose . . . kapena Aroni wamng’ono ndi iwo, akubwerera ku msewu, akulira. “Shi-shi-shi-shi-shi! Penyani izo.”

236 Ndipo Miriamu wamng’ono, iye wangoyimabe, akuyang’ana. Iye anati, “Oh! Oh!”

237 Anati, “Zibwera, Miriamu, kwayamba kucha. Zibwera, atambala akulira. Zibwera, kwayamba kucha. Zibwera, wokonedwa, tiye tizipita!”

238 Anati, “Oh, adadi, adadi! Chonde, kamodzinso. Ndiloleni ine ndingoyima, mungondilola ine ndimuwone iye ndipo mungondilola ndiwone chimene chitachitike. Ine ndibwerera kunyumba pakapita kanthawi.”

239 “Oh,” [M’bale Branham akukhwatchitsa chala chake—Mkonzi.] “limenelo ndi lingaliro labwino, Miriamu. Izo zikhoza kukhala zabwino. Iwe ungoyima ndi kuwona chimene chitachitike.”

“Chabwino, ine—ine ndizimuwona iye.”

240 “Tsopano, iwe ufulumire kubwera kunyumba pakapita kanthawi. Iwe ungowona chimene chitachitike. Ndipo uzibwera, utibweretsere ife nkhu, chimene chikuchitika.”

“Chabwino, adadi.” Ndipo iwo anachokapo, amayenera kuti afulumire.

241 Miriamu wamng’ono, iye akuyima ndipo iye akuwona. Chinthu choyamba inu mukudziwa, kwayamba kuwala. “Oh, oh, oh, ndi chiyani chikubwera kumeneko? Ndi—ndi chidutswa. Ayi. Kodi ndi ng’adzi? Oh, iye anapotoloka.”

242 Ha-ha! Kodi iye anawona chiyani? Iye akuwona chimene anthu ambiri samachiwona. Mukuona? Katundu wamng'ono ameneyo anali akuyenda, akuyandama pamenepo. Iwo ankaganiza kuti iye analibe woyendetsa; iwo ankaganiza iye analibe wamkulu aliyense. Iye anali naye. Iwo atasonkhana mozungulira ponsepo.

243 Apa pakubwera ng'ona yaying'ono, ikuti, "Oh, onani pamenepo!" Apa iyo ikubwera, ikuyandama monga *choncho*. Iye anapita... Oh, ayi. Ayi, ayi. Iye sangayandikire katundu ameneyo.

Mmenemo munayima womasula, muwomboli, Ayuda firii miliyoni amene ankafuna kumasulidwa. [M'bale Branham akugogoda pa guwa kasanu—Mkonzi]. Adierekezi onse mu gehena sakanakhoza kumugwira iye. Chikuyandama, chombo chaching'ono ichi chopangidwa ndi phula, chikuyenda mu mtsinje.

244 Chinthu choyambirira inu mukudziwa, icho chikulowa mu dziwe la madzi ozungulira. "Oh!" Miriamu anati, "Oh! Oh! Taonani icho! Limenelo ndi dziwe la madzi ozungulira, tachiwoneni icho! Tachiwoneni icho monga *choncho*!" Chinthu choyamba inu mukudziwa, zonse pakamodzi icho chinasuntha.

245 Umo ndi mmene izo zimakhalira. Ife timalowa mu dziwe la madzi ozungulira, nthawizina, khungwa laling'ono ili. Musadandaule. Pali Winawake akuyang'ana. "Angelo a Mulungu amazungulira iwo amene amamuwopa Iye." Ali ndi teni sauzande a iwo ali pa mndandanda wa oguba tsopano.

246 Miriamu wamng'ono, iye akupita kumeneko, iye akukwera pa thanthwe lalikulu ili, ndipo akukhala pa ilo monga *chonchi*. Ndipo akuthamangirako, iye akuyang'ana chombocho. Ndipo akutsikirabe kumusi kudutsa *apa*, ndi kudutsa mulu uwu wa mbendera. Patapita kanthawi icho chakodwa kumeneko. Akuti, "Oh! Oh, ine ndikudabwa!"

247 (Tsopano, abambo ake anamuza iye, anati, "Tsopano usalole aliyense akuwone iwe ukuchiyang'ana icho. Ngati winawake angabwere, ungopanga ngati kuti sukuyang'ana pa icho nkomwe, ungopita njira yina. Usati—usakachite ngati kuti ukuyang'ana nkomwe, uzikangopitirira chitsogolo." "Chabwino," iye anatero.)

248 Iye akupita mmphepete. Icho chakodwa. Chinthu choyamba inu mukudziwa, pali gulu lalikulu la asodzi. Ndipo iye akungopanga ngati kuti ndi mtsikana wamng'ono amene akungoyenda kumeneko. Akupita, teni koloko masana tsopano, inu mukudziwa, chotero iye ankangoyenda kumatsika ndi mtsinje. Ndipo akungoyika diso lake mmbuyo, chammbali, kuti awone kumene icho chikupita.

249 Patapita kanthawi iye akudutsa gulu lina. Akungopitirira kumayang'ana; akupita patsogolo pang'ono. Akupitirirabe kumapita, akupita patsogolo pang'ono.

250 Patapita kanthawi iye akufika pa khoma lalikulu. "Oh, mai, icho chikupita kuseri kwa khoma ili!" Iye angachite chiyani? Iye sakudziwa choti achite. Chotero iye sangapite kuseri kwa khomalo, chotero iye akungolowa mmadzi ndi kukayima pafupi ndi icho monga *chonchi*, ndi kukwawira pamwamba. Iye akupita pamenepo, ndipo akungoyendabe.

251 Chinthu choyamba inu mukudziwa, iye ali mmunda wokongola. Maluwa akuphukira paliponse, ndipo iwo ndi okongola kwambiri. Tsopano mvetserani mphindi chabe. Tsopano taonani, atsikana achichepere. Maluwa okongola, ndipo, oh, mitengo yonse itaduliridwa. Iwo amawoneka okongola! Ilo ndi bwalo lochezera. "Oh," iye anati, "taonani uko, icho! Oh, mai! Ine ndiri pabwalo la nyumba ya chifumu, nyumba yachifumu ya Farao, pa bwalo. Ine ndichita chiyani kuno? Ngati iwo angandipeze konse ine kuno, oh, mai, iwo achita nane chiyani ine?"

252 Ndipo iye akuyang'ana. Pamenepo chikupita chombo chaching'onocho, ndipo icho chikukhala ngati chayima kumeneko mmadzi, ndipo chikuyamba kuyandama mozungulira, chikuchoka mmadzi. Ndikudabwa chifukwa chiyani. Ndipo iye akumumva winawake akuyankhula. Iye akukabisala pansu pa tchire. Iye akukhala pansu, ndipo akuyang'ana kunja monga *choncho*, inu mukudziwa, Miriamu wamng'ono akuyamba kuyang'ana kunja, kuti achiwone icho.

253 Chinthu choyamba inu mukudziwa, apa pakubwera amuna ena aakulu akuda amphamvu atanyamula ambulera mmwamba monga *chonchi*. Ndipo antchito akuwatsatira, ndipo iwo akuyimba. Ndipo apa pakubwera mkazi, ndipo iye ali ndi chibangiri chachikulu cha golide mozungulira pa mutu pake, ali ndi njoka yayikulu itayasamula kamwa lake (monga *choncho*) kutsogolo kwake. Ndipo iye ndi mkazi wowoneka bwino, ndipo iye akubwera kumeneko. Iye wavala zovala zokongola, ndi zinthu. Ndipo ine ndikumumva mmodzi wa antchito akuti, "Mfumu yathu, inu mukuganiza kuti madzi akhala otentha mmawa uno?"

254 Miriamu anati, "Mfumu? Oh, izo ziyenera kukhala zachifumu, chotero ndiyenera kukhala kuti ndiri pa bwalolo. Ndipo ngati iwo atandigwire ine kuno, iwo achita nane chiyani ine?"

255 Chabwino, iye akubwera kumeneko, ndipo amuna aakulu akuda awa atanyamula pholo monga *chonchi*, akuyenda kumusi mmbali mwa madzi monga *choncho*, ndipo iye akuvula nsapato zake. Ndipo wantchito wina anali ndi zopukutira, ndipo ena anali ndi sopo. Ndipo iye amapita kuti akakhale ndi kusamba

kwa mmawa. Chotero iye akupita kumusi uko ndipo akuyamba ku—kukonzekera kusamba kwake. Iye akuvula nsapato zake. Iye anati, “Ndiyika zala zanga mmadzi ndi kuwona ngati iwo akutenthabe. Oh, iwo ali abwino basi, basi. . . Ndi chiyani icho uko?”

²⁵⁶ “Oh!” Miriamu, Miriamu wamng’ono anati, “Oh! Uh—oh, iye wazonda kale chombocho.”

“Oh,” iye anati, “kodi iyo ndi ng’ona?”

²⁵⁷ Mmodzi wa amuna aakulu amphamvu amenewo anati, “Miniti chabe, ine ndifufuza.” Kupaza, kupaza, kupaza, akuyenda kulowa mmadzi. Akunyamula icho monga *choncho*, ndipo akulowa. Anati, “Mfumu yanga!” Akuchipereka icho kwa wantchito. Ndipo wantchito akutenga ndipo akukachipereka icho kwa iye monga *choncho*, ndipo akukachikhazika icho pansu.

²⁵⁸ Iye anati, “Icho ndi chiyani? Psyii, chikununkha! Chiri ndi phula paliponse. Onani apa, chiri ndi bowo pamwamba pake.”

²⁵⁹ Ndipo Miriamu anati, “Oh! Oh, apo pakupita mchimwene wanga wamng’ono! Apo pakupita mchimwene wanga wamng’ono!”

²⁶⁰ Ndipo chotero iwo akutsegula icho monga *chonchi*. “Oh, anali mwana!” Ndipo iye anayamba. . . Mwana wokongoletsetsa mdzikoli! Ndipo, oh, Mulungu Amene angayambitse chidani, akhoza kuyambitsa chikondi; ndipo chikondi chonse chimene Iye akanayika mu mtima wa munthu, mayi kwa mwana, Iye anachiyika mu mtima wa mtsikana ameneyo. Ndipo iye—iye anati, “Ndi mmodzi wa Aheb-. . . Ine ndikudziwa chimene icho chiri. Ndi bambo woyipa wa ine uja ameneyo! Iye ndi wankhanza kwambiri! Iye walamula kuti ana onse Achihebri apshedwe. Ndipo mmodzi wa amayi amenewo wangomutaya mwana wake, akuyembekezera kuti iye akakocheza kulikonse kumene angathe. Oh, iye ndi woyipa! Chabwino, iye samupha uyu, chifukwa uyu ndi wanga.” Uh—huh, mukuona mmene Mulungu akuchitira?

²⁶¹ Iye anamunyamula iye, ndipo [M’bale Branham akupanga phokoso lopsyopsyona—Mkonzi.] akumupsyopsyona iye. Ndipo mwanayo analira. Ndipo pamene iye analira, izo zinangotentsetsa mtima wake. Iye anati, “Kanthu komvetsa chisoni kakang’ono.” Anati, “Ndimutenga iye ndipo ndimutcha iye. . . Ine ndimupatsa iye dzina.” Ndipo pamenepo ndi pamene iye anapezera dzina lake.

²⁶² Dzina lake anali ndani? [Osonkhana akuti, “Mose.”—Mkonzi]. Mose. Ndipo *Mose* amatanthauza “kutengedwa kuchokera mmadzi.” Mukuona?

²⁶³ Iye anati, “Tsopano ine ndimutcha iye Mose, ndipo iye adzakhala mwana wanga yemwe. Ine ndimusunga

ieye. Koma tsopano,” iye anati, “koma ine ndine namwali sindingamuyamwitse iye. Ine—ine—ine ndiribe njira iliyonse yomudyetsera iye.” Iwo analibe mabotolo awa ndi zinthu nthawi imeneyo. Akazi sankasuta ndudu mmene akuchitira tsopano, inu mwaona, ndi kumadzipatsa okha chiphe. Chotero anati, “Chabwino, ngati iwe ukumudziwa a . . .” Anati, “Chiyani—ine ndichite chiyani?” Chotero iye anati, “Ine . . .”

264 Mmodzi wa iwo anati, “ine ndikuuzani inu, mfumu, ine ndikamupeza mayi woyamwitsa wa mwana wanuyu.”

“Oh,” iye anati, “izo ndi zabwino kwambiri.” Wachichepere . . .

265 Chinachake chinayankhula, Mngelo atayima pamenepo patchire, anati, “Miriamu, mwayi wako ndi umenewo! Mwayi wako ndi umenewo!” Miriamu wachichepere anathamanga. Anati, “Usanene kanthu tsopano, iwe usazisiye. Iwe upite kunjwa ndipo ukanene kuti ‘umpeza woyamwitsa,’ ndipo upite ukawatenge amayi ako.”

Chabwino, chotero iye ananena izo. Iye anati, “Mfumu!”

266 Tsopano, mwawamba, iye akananena, “Iwe ukupanga chiyani kuno?” Koma, mwaona, Mulungu anali akuziphimba zonsezo. Bwanji? Iye anali ndi Angelo teni sauzande akuguba. Mukuona? Dongosolo lake litheka. Iye anali ndi Angelo teni sauzande atayima pamenepo.

267 Chotero chinthu choyamba inu mukudziwa, anati, “Anu . . .”

Anati, “Inde, wokonedwa wamng’ono, iwe ukuchita chiyani kuno?”

268 Iye anati, “Ine ndangokuwonani inu ndi mwana.” Anati, “Ndikudziwa kumene kuli mayi wabwino amene angakusamalireni mwana wanu.”

269 Iye anati, “Pita, ukamutenge iye, ndipo ukamuze iye kuti ndizimupatsa iye madola firii handirede pa sabata kuti azimusamalira mwana uyu, ndipo ine ndimupatsa iye chipinda chathunthu ku nyumba yachifumu. Ndipo ngati iwe ukudziwa kumene kuli mzimayi wa Chihebri, amene ndi woyamwitsa, amene angakhoze kumuyamwitsa mwana uyu, uyu ndi mwana wanga.”

Anati, “Inde, mfumu, ine ndikakupezerani mmodzi.”

270 Anati, “Tsopano, dikira miniti! Iwe usanapite ku nyumba yachifumu, ukuyenera kukhala ndi dzina lachinsinsi. Mwaona, iwe sukudziwa dzina lachinsinsi. Tsiku lililonse timakhala ndi dzina lachinsinsi. Tsopano, dzina lachinsinsi lero, iwe ukudziwa chimene ilo linali? ‘Foroko ndi mulu wa msipu.’” Anati, “Izo ndi zimene iwe ukuyenera kukanena kuti udutse pachipata.”

271 Chotero Miriamu wachichepere akuchoka kupita kunyumba, molimba momwe iye angathere, ndi kudumphapha

khoma, kumatsika ndi msewu, ndi kumatsikira mbali *iyi*, ndi kutsikira mbali *iyi*, ndipo molimba momwe iye angathere. Iye anathamanga kukalowa mnyumba.

²⁷² Ndipo—ndipo Amram anali atangofika kunyumba, ndi Jochebed. Ndipo, oh, iwo anali okhumudwa, akulingalira chimene chikuchitika. Iye anati, “Mwana wanga wosauka! Mwana wanga wosauka!” Iye. . .

²⁷³ Iye anati, “Tsopano tangomvetsera.” Anati, “Ine ndimangodutsa kumene kamphindi kapitako kumusi uko pa msewu, ndipo mayi wosauka uyo wapangitsa aliyense kukhala maso tsiku lonse. Iwo anabwera kudutsa mu dera lino mmawa uno, ndipo anaphulitsa mutu wa mwana aliyense amene analipo mu derali.” Ndipo anati, “Momwe iwo amafuulira ndi kulira! Tsopano, sindikudziwa, mwana wako, kulikonse kumene iye ali. Kumene mwana wathu ali, Mulungu amusamalira iye.”

²⁷⁴ Basi pomwepo chinachake chinapita. . . [M’bale Branham akugogoda pa guwa kanayi—Mkonzi]. “Oh! Oh! Ndi awo pamenepo, pa chitseko tsopano.” Chotero, iwo anapita ndi kukayang’ana. Ayi, sindiwo. Anali Miriamu.

²⁷⁵ Iye anati, “Oh! Oh, Miriamu! Lowa, wokondedwa! Chachitika ndi chiyani kwa mwana?”

Iye anati, “Amayi, ine ndiri ndi njala.”

Anati, “Koma chachitika ndi chiyani kwa mwana?”

²⁷⁶ Anati, “Ine ndiri ndi njala, amayi.” Anati, “Oh, Ambuye alemekezeke! Aleluya! Ine ndiri ndi njala, amayi.”

Anati, “Koma chachitika ndi chiyani kwa mwanayo?”

²⁷⁷ Anati, “Amayi, ndiri ndi njala kwambiri mwakuti ndikhoza kudya chirichonse chiri mnyumba muno.”

²⁷⁸ Anati, “Tikupezero chinachake choti udye, koma chachitika ndi chiyani kwa mwanayo?” [M’bale Branham akugogoda pa guwa katatu—Mkonzi].

²⁷⁹ Anati, “Oh, mwana ali bwino bwino, amayi. Ndipatseni chinachake choti ndidye. Oh, ndine wokondwa kwambiri!”

“Koma chachitika ndi chiyani kwa iye?”

²⁸⁰ “Chabwino, ndipatseni chinachake choti ndidye, ine ndiri pafupi kufa ndi njala.” Inu mungaganizire zimenezo?

²⁸¹ Iye anati, “Miriamu! Awa ndi amayi ako ndi abambo. Mwana ali kuti?” [M’bale Branham akugogoda pa guwa katatu—Mkonzi].

²⁸² Iye anati, “Amayi, ine ndakuuzani inu. Mwanayo, ine ndamuwona iye, ndipo iye ali bwino bwino. Tsopano, amayi, ndipezereni chinachake choti ndidye; ine ndikufa ndi njala. Inu mukudziwa, ine—ine ndiri pafupi kufa ndi njala.” Monga momwe inu mumachitira pamene mwabwera kunyumba

kuchokera ku sukulu, inu mukudziwa; oh, inu mumayenera kukhala ndi chinachake.

Chotero, iye anapita ndipo anakamutengera iye sangweji. Anati, “Tsopano ndiuze ine.”

²⁸³ Ndipo iye akumveka, “Yamu, yamu, yamu,” akudya, inu mukudziwa, chomwecho. Anati, “Amayi?”

Anati, “Inde, koma chachitika ndi chiyani kwa mwanayo?”

²⁸⁴ “Bwanji,” anati, “amayi...” Iye anawafotokoza iwo nkhani yake. Ndipo anati, “Amayi, inu mupite mukatenge zovala zanu zapamwamba, ndipo mulongeze mchikwama chanu, chifukwa inu mukupita kukamusamalira mwanayo.” Oh! Oh! Oh!

“Chiyani?”

²⁸⁵ Ngati mumutaya iye, inu mudzamupeza iye kenanso. Nkulondola uko? Ngati mumusunga iye, inu mudzambutaya iye. Ngati mungampereke iye, kumutaya iye, mudzamupeza iye. Nkulondola uko?

²⁸⁶ Ndipo Miriamu wamng’ono akungodya. Anati, “Inde.” Anati, “Inu mukupita ku nyumba yachifumu lero. Ndipo osati zokhazo, koma inu mukupita, mwapatsidwa, muzikapatsidwa madola firii handirede pa sabata, ndi zipinda zapamwamba mfukoli, kuti muzikamusamalira mwana wanu yemwe.”

²⁸⁷ Nthawi yoyamba mu mbiri yakale yonse ya mdziko pamene mayi analipiridwapo kuti azimusamala mwana wake yemwe. Mukuona momwe Mulungu amachitira izo? [M’bale Branham akuwomba mmanja ake katatu—Mkonzi]. Aleluya! Kumuyamwitsa mwana wake yemwe, ndipo nkumalandira madola firii handirede pa sabata chifukwa chotero, ndi zipinda zapamwamba mdziko. Mulungu amachita zinthu, sichoncho Iye? Kodi zimapindulitsa kupemphera? [Osonkhana akuti, “Inde.”] Kodi ndikwabwino kupemphera? [“Ameni.”]

²⁸⁸ Chotero, iye anakonzekeretsa chikwama chake. Ife tifulumira tsopano, ife titseka mu miniti. Chotero ife... Iye anakonza chikwama chake, ndipo akutsika msewu iye anapita, mwamphamvu mmene iye akanathera. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, iye akubwera; mlonda wamkulu atayima pamenepo ndi nthungo yake yayikulu, anati, “Ndani akupita pamenepo?”

Iye anati, “Foroko ndi mulu wa msipu.”

“Dutsani.” Mukuona momwe Mulungu amachitira zinthu?

²⁸⁹ Anapita kwa mlonda wotsatira. Pamenepo iye anasolola lupanga lake, anati, “Iwe ndi ndani? Ndani akupita pamenepo?”

Anati, “Foroko ndi mulu wa msipu.”

Anati, “Dutsani.” Mai! Mukuona momwe Mulungu amachitira zinthu?

290 Akukwera mmwamba, akupita akuyang'ana mnyumba yachifumu; akuyamba, ndipo achifumu onse akutuluka, akusolola malupanga awo. “Ndani akupita kumeneko?”

Anati, “Foroko ndi mulu wa msipu.”

“Dutsani mulowe.”

291 Chinthu choyambirira inu mukudziwa, mwamuna anatuluka, anati, “Kodi ndiwe dona wamng'ono amene mfumu akumudikirira?”

“Inde.”

292 “Ndipo uyu ndiye woyamwitsa mwana amene wapezeka mmawa uno?”

“Inde.”

293 Anati, “Chabwino, mubweretse iye alowe.” Chotero iye akumulowetsa mwanayo . . . kapena akuwalowetsa amayiwo.

294 Ndipo—ndipo—ndipo mfumukazi wamng'onoyo anatuluka, ndipo anati, “Kodi iwe umadziwa chirichonse chokhudza ana?”

Iye anati, “Inde, mfumu.”

Iye anati, “Tamuwone mwana uyu. Iye si wokongola?”

“Inde, mfumu. Inde.”

Anati, “Kodi iwe ungadziwe kumuyamwitsa mwanayu?”

“Inde, mfumu. Ndithudi.”

295 “Chabwino,” iwo anati, “Ine ndizikupatsa iwe, malipiro ako ndi, madola firii handiredede pa sabata.” Hum! Mulungu Sanali wabwino? Ndipo anati, “Ndipo iwe uli ndi zipinda zapamwamba mnyumba yachifumu, ndipo zakudya zako ziziperekedwa kwa iwe. Iwe sumasowa kuti uzituluka ndi kumadzaphika zakudya zako.” Anati, “Tsopano, mwanayo ndi uyu, umusamale. Usamugwetse iye.”

“Oh, musadandaule, ine sinditero. Musadandaule, ine sindimugwetse iye.”

“Iwe uzimusamalira bwino iye.”

296 “Musadandaule, ine nditero. Iye akhala ndi chisamaliro chapamwamba kwambiri.” Ndithudi, iye anali wake yemwe, mwaona. “Ine ndimupatsa iye chisamaliro chapamwamba kwambiri.”

“Iwe ukuwona iye ndi mwana wokongola?”

“Wokongola kwambiri,” iye anatero.

“Chabwino.”

297 Chinatsekeka chitseko, pa Miriamu, ndi amayi ake, ndi Mose wamng'ono. Ndipo pamene chitseko chinatsekedwa, iye anayang'ana mozungulira paliponse. Iye anati, “Tsi-tsi-tsi! Ndipo iye amaganiza kuti iwe ndi mwana *wake*. Ha-ha-ha-ha-ha!” Oh, mai! Iye anamusamala iye.

298 Kodi iye anachita chiyani? Iye. . . Ngati iye akanamusunga iye, iye akanatani? [Osonkhana akuti, “Akanamutaya iye.”—Mkonzi]. Chifukwa, iye anamupereka iye kwa Iye Amene anamupereka iye kwa iye, ndipo iye (chiyani?) anamupeza iye, ndipo iye akhoza kumusunga iye. Tsopano chimachitika ndi chiyani tikataya. . . Ngati tisunga solo yathu, chimachitika ndi chiyani? [“Ife tidzaitaya iyo.”] Ife tidzaitaya iyo. Ndipo ngati ife tingayipereke iyo kwa Iye Amene anaipereka iyo kwa ife, chidzachitike ndi chiyani? [“Ife tidzaisunga iyo.”] Ife tidzaisunga iyo. Nkulondola uko?

299 Ndi angati a inu nonse amene angakonde kubwera mozungulira guwa ndi kudzapemphera? Inu mungakonde kuchita zimenezo? Kodi mungakonde kuti Yesu akusamalireni inu monga Iye anachitira ndi iwo, mwanayo? Motani. . . Tiyeni tonse, ana aang’ono, tisonkhane kuzungulira guwa apa tsopano. Kodi inu mungachite izo? Bwerani mudzazungulire, mudzagwade kuzungulira guwa. Tiyeni tipemphere, aliyense wa inu. Ana nonse bwerani tsopano kuno. Kodi inu munaikonda nkhani yanga ya izi? [Osonkhana akuti, “Inde.”—Mkonzi]. kodi inu munaikonda iyo? Chabwino, tsopano mubwere mudzazungulire guwa. Tsopano bwerani. Ana nonsenu bwerani, mudzagwade kuzungulira guwa, ingogwadani pansu pamenepo pa—pamenepo pa guwa. Ndi zimenezotu. Ana nonsenu kumbuyoko, bwerani kuno tsopano, ife tipemphera. Chabwino. Inu mukufuna kubwera ndi kudzapemphera. Kazibwerani ndipo mudzagwade kuzungulira guwali. Uko nkulondola. Tsopano, zimenezo ndi zabwino. Izo ndizabwino basi.

300 Tsopano, amayi, inu mukufuna kubwera, nanunso, ndi abambo, inu nonse mukufuna mudzagwade mkanjira?

301 Tsopano ndikufuna ndikufunsemi inu ana chinachake apa. Taonani. Kodi inu mukukhulupirira kuti Yesu amakukondani inu monga Iye anachitira ndi Mose? Inu mukukhulupirira kuti Angelo amakuyang’anirani inu monga chonchi? Tsopano, Mulungu anakupatsani inu solo, Iye sanatero? Tsopano, ngati muisunga solo yanuyo, chidzachitike ndi chiyani kwa iyo? [Ana akuti, “Tidzaitaya iyo.”—Mkonzi]. Mudzaitaya iyo. Koma ngati mungaipereke iyo kwa Yesu mmawa uno, ndiye inu mudzachita chiyani? [“Muisunga iyo.”] Mu—muisunga iyo. Inu mukufuna kupulumutsa. Tsopano inu mukufuna kupulumutsa solo yanu, inu simukutero? Ndipo inu mukufuna mudzakule kudzakhala amayi enieni ndi madona enieni, sichoncho inu; ndi mwamuna weniweni, alaliki, ndi zina zotero? Kodi inu simukufuna kuchita zimenezo? Tsopano, ngati inu mungatero, ndiye mupereke solo yanu kwa Yesu. Njira yake ndi iyi imene inu mungachitire izo. Inu munene, “Wokonedwa Yesu, izi ndi zonse zimene ine ndikupereka kwa Inu, ndi solo yanga, koma Inu muzindiyang’anira ine monga Inu munachitira ndi Mose.”

302 Tsopano, ngati ena a inu akuluakulu mukufuna kubwera ndi kudzagwada, nanunso, ena a inu amayi, mwinamwake, amene mukufuna kudzagwada kuno mmawa uno. Chabwino, izo ndi zotseguka kwa inu, nanunso. Ngati inu mungathe, bwerani, dzagwadani limodzi apa. Izo ndi zabwino. Apa pali amayi akubwera ndi mnyamata wawo. Wina angabwerenso?

303 Abambo, adadi, aliyense wa inu, ngati inu mukufuna kukhala mwamuna wopemphera momwe Amram analiri, inu mubwere, mudzagwade, nanunso.

304 Amayi, ngati inu mukufuna kuti mukhale monga Jochebed, bwanji, inu mubwere, mudzagwade, nanunso.

305 Ndithudi, izo ndi za aliyense. Chifukwa (Chiyani?) inu muli ndi solo, nanunso. Ngati inu mungayisunge iyo, chidzachitike ndi chiyani? [Osonkhana akuti, “Tidzaitaya iyo.”—Mkonzi]. Tidzaitaya iyo. Ndipo ngati inu mungaiperekenso iyo kwa Iye Amene anaipereka iyo kwa inu, chidzachitike ndi chiyani? [“Kuipulumutsa iyo.”] Inu mudzaipulumutsa iyo, ku Moyo wosatha. Uko nkulondola. Tsopano, kodi inu simusonkhana mozungulira, nonsenu amene mungathe tsopano, ndipo tiyeni tikhale ndi pemphero ndi aang’ono awa, ndi ife, ndi tonsefe tsopano.

306 Tsiku la Anakubala, tsiku lopambana. Ndipo mwinamwake usikuuno, ine ndikhoza kudzasintha phunziro langa ndi kupitirira usikuuno ndi kudzanena chimene mayi uyo anachita, momwe mayiyo anachitira. Iye anali amene anamuphunzitsa mnyamata wake wamng’ono kuti atsogolere Israeli yense kupita ku dziko lolonjezedwa. Oh, iye anali mayi weniweni. Kodi iye sanali mayi weniweni? [Ana akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Tsopano, inu muli ndi amayi enieni, nanunso, ndipo amayi akukupemphererani inu. Iwo anali abambo enieni. Ndipo abambo akukupemphererani inu. Ndipo tsopano ife tonse tipemphera pamodzi, ndi kumufunsa Yesu kuti atithandize ife.

M’bale Neville, kodi inu mungabwere, mudzagwade ndi ife?

307 Ndipo tiyeni tiweramitse mitu yathu, paliponse. Tsopano Mlongo Gertie... [Walimba akuyamba kuyimba *Abweretseni Iwo*—Mkonzi].

308 Wokonedwa Atate Akumwamba, nkhani yaying’ono, yophweka iyi lero, ya masiku amene anapita, pamene abambo ndi amayi owona, wokhulupirira woona, ankabwera kwa Inu ndipo anakupembedzani Inu. Iwo anakukhulupirirani Inu. Panali kupsyinjika mdziko pa nthawi imeneyo. Ndipo ife tidziwa bwanji kuti palibe Mose wamng’ono wamakono wagwada apa mmawa uno! Ife tidziwa bwanji kuti palibe Miriamu wamng’ono wamakono wagwada pano mmawa uno, aponso, mneneri wamakazi!

309 O Atate Wokonedwa, ana aang'ono awa amakukondani Inu, ndipo iwo abwera, adzagwada pa mtanda, akuzindikira kuti iwo ali ndi solo imene ikuyenera kupulumutsidwa, ndipo iwo akuyipereka iyo kwa Inu tsopano. Pakuti ife tangowerenga kumene mu Mawu Anu, “Ngati mungataye iyo, inu mudzayipeza iyo; ndipo ngati muisunga iyo, inu mudzaitaya iyo.” Ndipo, Atate, iwo sakufuna kusunga solo yawo kwa iwoeni. Iwo sakufuna kukhala moyo kwa iwoeni. Iwo akufuna kupereka solo yawo kwa Inu, kuti potero, popereka iyo, iwo adzapeze Moyo Wamuyaya. Perekani, perekani izi, Ambuye.

310 Adalitseni anyamata onse awa ndi atsikana kuzungulira guwa. Adalitseni amayi ndi abambo amene ali pano mmawa uno. Oh, mulole chisomo Chanu chokonda ndi chifundo zikhale pa iwo onse. Tikhululukireni ife, Ambuye, machimo athu onse ndi zolephera. Chotsani matenda pakati pathu.

311 Mutumize Angelo! Aleluya! Mulungu, Inu Amene munalamulira Gabrielo, ndipo Angelo teni sauzande anapita kukaguba, ndi Angelo angati owonjezera amene abwera pamene iwo awona ana awa atagwada pa guwa ili mmawa uno! Paliponse kuzungulira, pa guwa ili ndi kudutsa mtchalitchi chino, payima Angelo a Mulungu. Mngelo olembera ali pano, akulemba maina awo mu Bukhu. Iwo akuluza solo yawo, kuti iwo akathe kukaipeza iyo mwa Khristu! Perekani izi, Ambuye.

312 Mulole, kuyambira lero, mpaka mtsogolo, miyoyo yawo yaying'ono ikakhale yokoma ndi yodzichepetsa. Mulole iwo akakhale ana omvera kwa makolo awo ndi kwa Atate awo Akumwamba, kufikirira tsiku limene Inu mudzawayitanire iwo Kwathu. Atsogolereni iwo mu kachombo kawo kakang'ono, kudutsa mu dziwe la madzi ozungulira. Nthawi iliyonse iwo akakodwa mu tchire, mulole Angelo a Mulungu azikankhira icho kupita mu mphamvu zoyenda za chikondi cha Mulungu. Perekani izi, Ambuye. Ndipo pamapeto a njira, mulole iwo akapeze Nyumba yokoma, ndi amayi awo ndi okonedwa awo uko mu Ulemelero, kumene Mulungu amayima pa chipata kudzawalandira, tsiku limenelo. Perekani izi, Atate.

313 Tikhululukireni ife machimo athu onse ndi zolakwitsa. Ndipo tithandizeni ife kuyambira tsiku ili kuti tikhale Anu amphumphu. Tikuwapereka ana aang'ono awa mmanja Mwanu tsopano. Ndi amayi awa ndi iwo, Ambuye, kuti iwo akakhale amayi oyenera pa Tsiku la Anakubala ili, nthawi yachikumbutso iyi imene inaperekedwa kwa amayi. Ndipo mulole iwo, kuyambira lero, akhale amayi abwino. Mulole ana akhale ana abwino. Mulole ife tonse tikhale abwino, Ambuye, ndi kukutumikirani Inu mochuluka. Perekani izi, Atate, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Tsopano tiyeni tiyimbe kolasi yaying'ono.

314 Inu mukukhulupirira Yesu wakupulumutsani inu? Inu mukufuna Yesu azikuyang'anirani inu tsopano, pamene mukuimirira? Kwezani mmwamba dzanja lanu kwa Iye, monga *chonchi* tsopano. Ine ndikufuna inu mutembenukire kwa abambo ndi amayi, ndi onse a iwo. Tembenukirani mbali *iyi*. Tsopano penyani kuno, amayi ndi abambo. Atsikana nonsenu ndi anyamata imilirani. Tsopano, ndi angati mukumulandira Yesu ngati Mpulumutsi wanu, ndipo mumudalira Yesu kuyambira pano, kuti azikusamalirani inu monga Iye anachitira ndi Mose wamng'ono, tiyeni tiwone manja anu akupita. Aliyense wa inu. Izo ziri bwino! Tsopano chinachitika ndi chiyani? Ngati musunga solo yanu, inu mumatani? [Osonkhana akuti, "Umaitaya iyo."—Mkonzi]. Umaitaya iyo. Koma ngati iwe uyipereka iyo kwa Yesu, chidzachitike ndi chiyani? ["Uyisunga iyo."] Iwe udzaisunga iyo. Tsopano, nanga bwanji ngati Yesu ali ndi inu mmawa uno? Ndipo inu ndi a Yesu tsopano, inu simuli? Inu ndi mnyamata ndi mtsikana wa Yesu.

315 Tayang'anani pa anyamata awa ayima apa ali ndi misonzi. Mukundiiza ine kuti Mulungu sakudziwa zimenezo? Ameni. Amuna ndi akazi a mawa! Imirirani.

Abweretseni iwo kuchokera ku minda ya
tchimo;

Abweretseni iwo, abweretseni iwo,
Abweretseni aang'onowo kwa Yesu.

Oh, Momwe Ndinkondera Yesu, tsopano bwerani!

Oh,

Nonse a inu.

. . . momwe ndinkondera Yesu,

Tikweze manja athu mmwamba tsopano.

Oh, momwe ndinkondera Yesu,

Oh, momwe ndinkondera Yesu,

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine.

316 Kodi izo si zokongola? Tsopano, *Yesu Amakonda Ana Aang'ono A Mdziko Lapansi*. Tipatseni poyambira, mlongo. Tsopano inu nonse mutembenukira njira iyi, kwa ine, atsikana inu. Ine ndikufuna kuti ndiyimbe *Yesu Amakonda Ana Aang'ono A Mdziko Lapansi*. Ndi angati amaidziwa iyo? Chabwino, tiyeni tiyimbe tsopano.

Yesu amakonda ana aang'ono,

Ana onse a mdziko lapansi;

Ofiira ndi achikasu, akuda ndi oyera, iwo ndi
ofunika pamaso Pake,

Yesu amakonda ana aang'ono a mdziko
lapansi.

317 Tsopano, nonse a inu muli mu gulu la ankhondo tsopano. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Inu mukudziwa kuti muli mu

gulu la ankhondo a Mulungu? Tsopano, inu muzindiyang'ana ine tsopano. Ndipo muyimbe iyi ndi ine, chifukwa inu ndi asirikali tsopano. Kodi inu mukudziwa zimenezo? Asirikali a mtanda! Tsopano, *Ine Mwina Sindingagube*. . . Inu mukuidziwa imeneyo? Chabwino. Chabwino, kalekale, nyimbo yakale ya Sande sukulu ine ndinaiphunzira.

Ine mwina sindinga . . .

Tsopano inu, ndi ine tsopano. [M'bale Branham akupanga ziwonetsero pamene akuyimba *Ine Ndiri Mu Gulu La Ankhondo La Ambuye*—Mkonzi].

Ine mwina sindidzaguba ndi mwa chisirikali,
Kukwera pa hatchi, kumawombera zida
zankhondo;

Ine sindingauluke pamwamba pa mdani,
Koma ndiri mu gulu la ankhondo la Ambuye.

Ndiri mu gulu la ankhondo la Ambuye,
Oh, ndiri mu gulu la ankhondo la Ambuye!

Tiyeni pamodzi ndi ine tsopano. Tonse pamodzi tsopano. Tsopano!

Ine mwina sindidzaguba mwa chisirikali,
Kukwera pa hatchi, kuwombera zida
zankhondo;

Ine mwina sindingauluke pamwamba pa
mdani,
Koma ndiri mu gulu la ankhondo la Ambuye.

³¹⁸ Inu mukukhulupirira mukhoza kuyimba iyo panokha? Bwera kuno, mtsikana, bwera apa. Tsopano ndikufuna inu nonse muzichita momwe ine ndizichitira. Bwerani muzungulire, kuseri kwa guwa kuno, tsopano. Bwerani cha kuno. Aliyense wa inu, sunthirani kuno kumene ine ndiri, mwaona. Gubirani kuno; palibe amene atakhale kunja kwa guwa. Bwerani kuno ndi ine. Ndi zimenezotu. Kulondola. Monga *chonchi*. Tsopano tembenukani monga *chonchi*, muyang'ane kwa omvetsera awa, monga *chonchi*. Ndi zimenezotu. Ine ndikufuna ndikuwonetseni inu chimene anyamata ndi atsikana abwino amachita akamudziwa Yesu. Tsopano, bwerani kumbuyo kuno, anyamata ndi atsikana. Tsopano ndinu. . . Ndi zimenezotu. Tsopano onani kunja kumeneko.

³¹⁹ Tsopano pamene ine ndikuti, “Ine mwina sindidzaguba mu gulu la ankhondo,” inu. . . “kuguba mwa chisirikali,” inu mudziguba, nanunso. Pamene ine ndiziti, “Ine mwina sindidzakwera pa hatchi,” inu muzichita zinthu zomwezo zimene ine ndizichita. Tsopano mukhale kumbuyo monditalikira ine, kumbuyo tsopano, mupange malo. Kumbuyo, kumbuyo, tsopano inu mwakonzeka. Tsopano yambani, tiyeni tiyimbe iyo. [M'bale

Branham ndi ana akupanga ziwonetsero pamene akuyimba—Mkonzi].

Ine mwina sindidzaguba mwa chisirikali,
(Penyani!)

Kukwera pa hatchi, kuwombera zida
zankhondo;

Ine mwina sindingauluke pamwamba pa
mdani,

Koma ndiri mu gulu la ankhondo la Ambuye.

Oh, ndiri mu gulu la ankhondo la Ambuye,
Ndiri mu gulu la ankhondo la Ambuye!
(Konzekani!)

Ine mwina sindidzaguba ndi mwa chisirikali,
Kukwera pa hatchi, kuwombera zida
zankhondo;

Ine mwina sindingauluke pamwamba pa
mdani,

Koma ndiri mu gulu la ankhondo la Ambuye.

³²⁰ Amen! Mungoyima njii. Ndi angati akuzikonda zimenezo? Nenani, “Ameni.”

³²¹ Tsopano, Atate Akumwamba, adalitseni ana awa lero. Iwo ndi Anu, Ambuye. Iwo apereka miyoyo yawo kwa Inu. Iwo amva nkhani yaying’ono ya Mose ndi momwe Inu munamutetezera iye. Iwo amva za mayi wabwino ndi bambo wabwino amene anawathandiza iwo ndi kuwalera iwo. Ndipo chomwechonso ana awa ali ndi amayi abwino ndi abambo. Ndipo ine ndikupemphera, Atate, that Inu muwayang’anire iwo ndi kuwakondoweza iwo kutsikira ku mayendedwe a nthawi, ndipo mulole Angelo a Mulungu awatetezere iwo. Perekani . . . Ndiyeno mukhale ku mbali yolandira, kuti mudzawalandire iwo mmasiku otsiriza, Ambuye, kulowa mu Ufumu Wanu. Ife tikupempha mu Dzina la Khristu. Amen.

³²² Tsopano inu mukhoza kubwerera ku mipando yanu ndipo mukawauze abambo ndi amayi momwe inu mukumverera bwino. Amen.

³²³ “Masiku onse akuyendayenda kwawo iwo ankatsogoleredwa.” (Inu mukuidziwa imeneyo, inunso?)

. . . a kuyendayenda kwawo iwo
ankatsogoleredwa,

Kupita ku dziko lalonjezo iwo
ankatsogoleredwa;

Ndi dzanja la Ambuye mu chitsogozo ndithudi,
Iwo anabweretsedwa ku gombe la Kenani.

Aliyense!

Chizindikiro cha moto usiku,
 Ndi chizindikiro cha mtambo masana,
 Chikuyandama pamwamba, basi patsogolo,
 Pamene iwo ankayenda pa njira yathu,
 Namulondola ndi mtsogoleri adzakhala,
 Mpaka titadutsa mchipululu,
 Pakuti Ambuye, Mulungu wathu, mu nthawi
 Yake yabwino
 Adzatitsogolera ife ku kuwala pamapeto.

³²⁴ Ndi angati akudwala mmawa uno ndipo akufuna pemphero? Tiyeni tiwone dzanja lanu. Pokhala kuti tachedwa pang'ono, mwina mwake tisiya msonkhano wathu wamachiritso mpaka usikuuno, ndipo tingopemphera tsopano, chifukwa ife tachedwa pang'ono.

³²⁵ Kodi inu mwasangalala ndi nkhani yaying'onoyi? [Osonkhana akuti, "Ameni!"—Mkonzi]. Inu mukuganiza kuti izo zinali zabwino kwa anawo? ["Ameni!"] Eya. Ife—ife timawalambalala iwo nthawi zambiri. Ife tisamachite zimenezo. Mwaona, ine sindimapeza mwayi wophunzitsa Sande sukulu, ndipo mmawa uno inali nthawi yoti ndiyankhule kwa iwo. Ine sindimafuna kuti ndikutopetseni inu, koma ndimafuna kuti ndikuuzeni inu nkhani yaying'ono iyi.

³²⁶ Kumbukirani, ana aang'ono, imeneyo si nkhani yakale yaying'ono imene inu mumaiwerenga kulikonseko. Ndicho Choonadi. Ndicho Choonadi! Mulungu anachita zimenezo. Ndipo Iye ali ndi *inu* tsopano. Chabwino.

³²⁷ Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano pamene tikuyimba nyimbo yathu yobalalikira, pang'onopang'ono, "Tenga Dzina la Yesu ndi iwe, ngati chishango kwa mdani aliyense." Chabwino.

Tenga Dzinalo la Yesu,
 Mwana wa chisoni ndi wa tsoka.



KUPHUNZITSA ZA MOSE CHA56-0513
(Teaching On Moses)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, Meyi 13, 1956, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2023 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org